BUKHU

[LOMASULIRIDWA]

LA

CHIVUMBULUTSO

BUKHU 4
[CHAPUTALA 14 – 18]

Kwa
Mkwatibwi wa Khristu
Bukhu iri laperekedwa

BUKHU {LOMASULIRIDWA} LA CHIVUMBULUTSO

BEN HOWARD

Translanted To Chichewa Language
By

Enoch Kamanula
New Testament Assembly
P.O. Box 64
Mwanza-Malawi

KUSINDIKIZIDWA KOYAMBA 1980

KUSINDIKIZIDWA KACHIWIRI 2005

Palibe gawo la bukhu iri limene lingachulukitsidwe [kupatula lemba la Baibulo] popanda chilolezo cholembedwa. Kuti mumve zambiri lemberani ku:

Sound of Liberty
Ben Howard
7286 Hwy 53W
Dawsonville, Georgia 30534 (USA)
TwoAnds@soundofliberty.org
www.SoundofLiberty.org

MALONJE

Bukhu la Chivumbulutso ndi bukhu la zoimirira, limene; politanthauzira, ndi uneneri wapamwamba. Iri si bukhu limene likuchita ndi chiphunzitso kapena ziphunzitso za maziko zimene zinabwera kwa ife ndi mtumwi Paulo ndi alembi ena a malemba za m'mene tingapulumutsidwire kapena m'mene tingalandirire dongosolo la chipulumutso la Mulungu.

Bukhu la Chivumbulutso linalembedwa mu 96 A.D. mpingo utagwa ku chikondi chake choyamba. [Chivumbulutso 2:4] Chikuonetsa m'mene mpingo unathera kudutsa mu nthawi mu maonekedwe ake akugwa. Chikuonetsanso [ndipo mofunika kwambiri] mpingo ukubwezeretsedwa ku malo ake a pachiyambi kuno ku nthawi yotsiriza.

Mpingo wapachiyambi sunagwe kuchokera ku bukhu la Chivumbulutso, chifukwa sunali gawo la malangizo wolembedwa kwa mpingo kuchiyambi. Ndi bukhu la mwala wapangodya, ndipo osati bukhu la maziko, ndipo kotero ndilongomasuliridwa kwa mpingo pano pa nthawi yotsiriza. Ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa mkwatibwi, ndipo Khristu akupanga chikondi ndi mkwatibwi wake pamene Iye akumupatsa iye mzimu wa vumbulutso ndi kuulura zinsinsi kwa iye. Ichi ndi chifukwa cha bukhuli, **"Bukhu [lomasuliridwa] la Chivumbulutso."** Ndi Mulungu kuika Chisomo Chachikulu [Machitidwe 4:33] pa mpingo wake mkwatulo usanachitike.

Komanso, mundirole ndilankhule, kuti owerenga ambiri a bukhu la Chivumbulutso alakwitsa potenga Yohane, mlembi, ngati Yohane nkonzi wa bukhu. Koma palibe njira iriyonse tinganene molondora kuti Yohane ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso. Iye anali mlembi, chotengera chabe chimene Mulungu anagwiritsa ntchito kufalitsa malingaliro Ake ku Mau olembedwa kuti awuluridwe pano mu nthawi yotsiriza. Yesu anali, ndipo ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso.

Momwemonso olemba bukhu iri akuzindikira mochuluka kuti NKONZI wa bukhu la Chivumbulutso ndi amene wapereka kudzoza kwa kumasulira kwenikweni kwa mlembi uyu. Kotero, ine ndikupemphera kuti mwapemphero inu mutenga kumasulira kwa bukhu la Chivumbulutso chifukwa mkwatibwi wa Khristu adzamvetsa bwinobwino zimene zikuchitika pano mu nthawi yotsiriza, chifukwa kuwala kwake [kumvetsa] ndi kowala ngati krustalo. [Chivumbulutso 21:11]

Komanso, ndiloreni ndinene ine -Ben Howard- kuti: kwa zaka zoposa 45 ndakhala ndikutumikira pa zolembedwa zimene ziri mu bukhu iri, ngati mishonare mu maiko ambiri ndi kuno ku USA, mu mipingo, maholo, madera, nyumba zobwereketsa, ngati mlaliki wa pa wailesi, kufunsidwa mafunso, ndipo tsopano pa Internet, ngati m'busa wa **Sound of Liberty Assembly** moyandikana ndi Dawsonville, Georgia [USA] ndi mitundu ina ya malo wopezekamo anthu. Mwambiri mwa malo olankhulawa, kufunsidwa mafunso ndi zina, panali kujambulidwa matepi komanso kutenga mfundo zolemba pa zimene zimalankhulidwa zimene ine tsopano sindingathenso kuzilamulira.

- Kotero, zidziwike kwa onse: Kuti bukhu iri lapambana, ndipo laposa, zolembedwa zonse, zojambulidwa kapena mitundu ya nkhani zonse zotengedwa kuchokera kwa mlembi zimene zikuoneka ngati- kapena- zikutsutsana ndi zolembedwa izi, ngati zimenezo zinatengedwa mbuyomu lisanasindikizidwe bukhuli.
- Ichi ine ndikunena, chifukwa maulaliki ambiri pa matepi, ma CD, ma DVD, ma Video, komanso pa Internet apita ku madera ambiri padziko lonse kwa zaka zambiri zimene muli zochepa, ndipo mauthenga ena akale akhoza ngakhale kutsutsa zolemba izi, ine ndachita monga 2 Petro 3:18 amatiphunzitsa ife kuti *"Kukula mu chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu."*
- Kotero, ine ndinena kwa inu kuti ine ndakhala mu utumiki uwu kwa zaka zambiri, monganso inu amene mukuwerenga ichi kwa nthawi yoyamba, kuti bukhu iri lidzapereka kuwala kwakukulu ku "Bukhu la Chivumbulutso" kusiyana ndi mauthenga anga akale amene inu mukhoza kukhala nawo, kaya pa tepi, kulembedwa mwa bukhu, kapena zolemba zanuzanu pa zimene mlembi anapereka, kaya zaka 45 zapitazo kaya zaka 5 zapitazo.
- Ichi ndikunena, chifukwa mzimu womwewo wa Chivumbulutso umene unamupangitsa Yohane kulemba Bukhu la Chivumbulutso wapangitsa kuti limasuliridwe pano mu nthawi yotsiriza kwa Mkwatibwi Wake.

Izi ndikulankhula mokhudzana ndi bukhu lonse la Chivumbulutso, ndipo sirinapangidwe pa cholinga chochotsapo vumbulutso lirilonse limene Mulungu akanapereka patsogolo kwa ine kapena wina aliyense wa atumiki woona wa Mulungu pa Bukhu la Chivumbulutso. Inu mukhoza kukhala otsimikizika kuti vumbulutso lenileni siridzatsutsana ndi zolemba izi.

Posachedwa, utumiki onse woona udzaoneka diso kwa diso [1 Akorinto 1:10] pa kumasulira uku pamene liwu la vumbulutso la Mulungu liyamba kulankhula kuchokera kumwamba mu kufotokoza kwakukulu mwa Mzimu Wake [Chivumbulutso 10:8] pa zinthu zimene mukufuna muwerenge.

Ndikupempheni inu owerenga, kuti muzindikire kuti zolembedwa izi ndi za okhawo amene ali ndi makutu auzimu kuti amve chimene Khristu akunena kwa mkwatibwi wake pamene Iye akupanga chikondi ndi iye, chifukwa Bukhu la Chivumbulutso ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa Mkwatibwi.

Kotero, mukatha kuwerenga bukhu iri, ngati siringadzutse wamkati wanu ndi kuwalira moyo wanu, ndiye pepani potenga nthawi yanu, ndipo chonde perekani bukhu iri kwa wina aliyense chifukwa chowaganizira mwa pemphero, mwina ndi lawo. Ine ndikukuthokozani mokoma chifukwa cha nthawi yanu ndi mgwirizano.

Pemphero langa kwa inu owerenga ndi iri: *Mulungu akupatseni inu mzimu wa nzeru ndi chidziwitso, ndi kuti maso akumvetsa kwanu awunikiridwe. Kuti mukamvetse masamba otsatira a bukhu iri. Bukhu iri likuthandizeni kuti muvale chovala choyera [Chivumbulutso 19:7-9], kuti musandulike mkazi wa Khristu pokhala m'modzi ndi Mau Ake munthawi yotsiriza iyi. Amen.*

Kuthokoza Kwapadera Kwa …

Ine ndikufunanso ndiwonetsere kuyamikira kwanga pa
ntchito
ya malemu William M.Branham mneneri wa Mulungu
wam'thenga
wa m'badwo uno wa Laodikaya komanso malemu mtumwi
Raymond M. Jackson
amene Mulungu anamugwiritsa ntchito kuti apitirize ntchito Yake imene Iye anaiyamba kupyolera mwa William Branham; makamaka mu gawo la mbiri la bukhu iri. Ngakhale ife sitiri othandizidwa, kapena kukwezedwa ndi otsatira a
aliyense
wa uthenga wa amuna amenewa; zolemba zawo zinali zothandiza kwambiri pokonza bukhu iri.

Komanso, kuthokoza kwa padera kwa
Joyce Howard,
Gary Gentry,
Wanda Robertson,
Barbara Howard,
Leah Farruggia
ndi Enoch Kamanula
chifukwa cha kuthandiza mosatopa pa ntchito iyi.

"Ndipo anadza m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri, Nalankhula ndi ine, nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsera iwe…" Chivumbulutso 17:1.

Lemba la pamwambali likuonetsa m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri amene akulankhulidwa kudutsa mu bukhu lonse la Chivumbulutso. M'modzi wa iwo akumuonetsa Yohane, amene akuimirira utumiki ngakhalenso kuimirira mkwatibwi, bukhu la Chivumbulutso. Kuona angelo asanu ndi awiri ndi kumvetsa ntchito zawo zimene iwo amachita ndi zinthu zopindula ku kumvetsa kwanu ku bukhu la Chivumbulutso. Izi zatsimikizidwa mu bukhu lonseli ngati chifungulo chenicheni chotsekula zinsinsi za [zoyamba] bukhu lozwizwitsa la Chivumbulutso.
.

MALONJE KU CHAPUTALA CHIRICHONSE

Chaputala cha Khumi ndi chinai

Chaputala cha khumi ndi chinai chikuonetsera Ayuda 144,000 omwewo amene chaputala cha chisanu ndi chiwiri chikuonetsera, kungoti apa zalembedwa zimene iwo adzachita. **Awa 144,000 ndi gawo lotumikira la Israeli**. Iwo ndi woti alalikire uthenga wosatha ku pfuko lirilonse, mtundu wa anthu ndi manenedwe, ndi anthu mu zaka zitatu ndi theka zotsiriza za sabata la 70 la Danieli, ndi kuwatcha "obadwanso mwatsopano" kunja kwa mipingo ya zipembedzo.

Chaputala ichi chikuonetseranso Khristu akumasula mphamvu za uzimu kubweretsa kachitidwe kamene kangabweretse dzikolapansi ku nkhondo ya Armageddoni.

Chaputala cha Khumi ndi chisanu

Chaputala cha khumi ndi chisanu chikuonetsera miyoyo ya iwo amene anapereka miyoyo yawo chifukwa cha Mau a Mulungu, ataima pa nyanja ya mandala yosakaniza ndi moto. Awa ndi onse Ayuda ndi Amitundu amene aphedwa ndi chirombo. Chaputala ichi chikuonetsera kuti pa nthawi iyi Mulungu wakonzeka kutsanula chiweruzo Chake.

Chaputala cha Khumi ndi chisanu ndi chimodzi

Chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chimodzi chikuonetsera miriri isanu ndi iwiri, ngati chiweruzo chotsiriza cha Mulungu padziko Khristu asanabwere kudzayamba ulamuliro wa mileniamu. Miriri ndi yomveka bwino mu chaputala ichi.

Chaputala cha Khumi ndi chisanu ndi chiwiri

Chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chiwiri chikuonetsera Mpingo wa Katolika wa Chiroma pamene iye akukwera pa chirombo cha Kumadzulo kwa Ulaya. Chikutipatsanso ife mbiri ya Ufumu wa Chiroma ndikutionetsera kuti kumapeto, chirombo chomwecho chimene Mpingo wa Katolika ukukwera chidzamuukira ndi kumutentha iye pamoto. Uku ndi kumapeto kwa sabata la 70 la Danieli.

Chaputala cha Khumi ndi chisanu ndi chitatu

Chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chitatu chikuonetsera gawo la chiweruzo la utumiki la Ayuda 144,000 pamene iwo akuitanira chiweruzo pa Babulo. Mngelo pa vesi loyamba akuonetsera kudzoza kwa mphamvu ya Mulungu pa utumiki wao. 144,000 awa akutsutsa mipingo ya bodza ndi kutululutsa onse amene ali obadwanso mwatsopano chiweruzo chisanafike pa Babulo. Chaputala ichi chikuonetseranso zochitika za malonda za Mpingo wa Katolika wa Chiroma.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHINAI

Gawo Loyamba

Israeli ali ndi zaka zisanu ndi ziwiri za Mulungu zotsala kuchita ndi iwo mu uthenga wa chipulumutso. Aneneri awiri akubwera ndi kudzanenera zaka zitatu ndi theka zoyambirira. Iwo akuitana Ayuda 144,000 kuti alalikire Uthenga wa Wosatha mu zaka zitatu ndi theka zotsalira ndi kuitana chiweruzo kwa Babulo. **Utumiki wa 144,000 komanso gawo lachiwiri la chisindikizo chachisanu, zikuyamba ndi kutsiriza mu nthawi yofanana.** Izi zikutsiriza kanyengo kakang'ono kamene kakulankhulidwa ku Chivumbulutso 6:9-11 pamene zaka zitatu ndi theka zikutseka nyengo imeneyi.

Vesi 1: *"Ndipo ndinapenya, taonani, Mwanawankhosayo alikuimirira phiri la Ziyoni, ndipo pamodzi ndi Iye zikwi zana mphambu makumi anai kudza anai, akukhala nalo dzina lache ndi dzina la Atate wache lolembedwa pamphumi pao."*

Vesi 2: *"Ndipo ndinamva mau ochokera kumwamba, ngati mkokomo wa madzi ambiri, ndi ngati mau a bingu lalikuru; ndipo mau amene ndinawamva anakhala ngati a azeze akuimba azeze awo."*

Vesi 3: *"Ndipo ayimba ngati nyimbo yatsopano ku mpando wachifumu, ndi pamaso pa zamoyo zinai, ndi akulu; ndipo palibe munthu akhoza kuphunzira nyimboyi, koma zikwi zana mphambu makumi anai, ogulidwa kuchokera ku dziko."*

Vesi 4: *"Iwo ndiwo amene sanadetsedwa pamodzi ndi akazi; pakuti ali anamwali. Iwo ndiwo amene atsata Mwanawankhosa kuli konse amukako. Iwowa anagulidwa mwa anthu, zipatso zoundukura kwa Mulungu ndi kwa Mwanawankhosa."*

Vesi 5: *"Ndipo m'kamwa mwao simunapezedwa bodza; ali wopanda chirema."*

Chaputala cha khumi ndi chinai cha Bukhu iri la Chivumbulutso chagawidwa mu magawo atatu. Ife tangowerenga gawo loyamba limene likuchita ndi 144,000. Gawo lachiwiri likuchita ndi Uthenga umene akulalikira, nthawi imene akulalikira, ndi kuitanira chiweruzo pa Babulo. Gawo lachitatu likuchita ndi nthawi imene Mulungu akutseka m'bado uwu ndikusonkhanitsa mafuko palimodzi ku nkhondo ya Armagedoni. Ife tichita nazo mu magawo atatu. Mu masomphenya ake Yohane anaona Mwanawankhosa ndi 144,000 akutsatira Mwanawankhosa; ndipo anali ndi dzina la Atate wao pa mphumi zao. Kodi zimenezo zikutanthauza chiyani? Iwo alandira vumbulutso la chimene Yesu ali. Kodi dzina la Atate ndi chiyani? Ndi "Ambuye Yesu Khristu." Yesu anati, *"Ine ndinabwera mu dzina la Atate wanga."*

Pamene aneneri awiri akunenera, 144,000 awa akutenga vumbulutso la chimene Yesu Khristu ali. Iwo adzakhala gulu lapadera lodzozedwa la 144,000 limene liu la Mulungu lidzadzeramo mu ora limeneyo. Ngakhale kuti padzakhala Ayuda ena amene adzalandira chipulumutso pamene aneneri awiri adzanenera, gulu iri la144,000 limene lidzalalikira Uthenga wa Muyaya ndi *"Zipatso zoyamba kwa Mulungu ndi kwa Mwanawankhosa."*

Vesi lachinai likuti kuti awa sanadzidetsa ndi akazi. Kodi ndi akazi a mtundu wanji amene akutanthauza? Otchedwa mipingo. Zipembedzo izi sizingathe kukopa muyuda weniweni kuti uthenga wao ndiolondora. Pamene inu mupita kudziko la Israeli ndi kulankhula za chikhristu, iwo nthawi yomweyo amakuikani inu mu gulu la a Katolika kapena ena mwana ana chikazi a Chiprotestant, ndi mtundu wina wa uthenga wa utatu. Muyuda weniweni sangamvere zimenezo. Winawake anati kuti Ayuda ndi otsutsakhristu ndipo akuyenera kuphedwa, chifukwa sungathe kuwauza iwo chirichonse chokhudza Khristu. Pamene woyenera abwera, adzamva izo.

Dziko lino la Amitundu likanakhala mu mumaonekedwe abwino kwambiri lero ngati akanati asamvere za mkazi hule wakale ndi ana ake mahule. Anthu amakhala mu dongosolo la njira ya chipembedzo ndipo ndikovuta kuwagwedeza kuwachotsamo ndi Mau a Mulungu, koma apa pali 144,000 amene sanadetsedwe ndi kachitidwe aka ka uhule.

Ndiloreni ndigwetseremo izi mochuluka kuti muthe kudziwa chimene ndikutanthauza: monga m'mene kukhala namwali kukukhudzidwira, yense wa iwo sakanakwatira ndi kukhala ndi ana ochuluka. Izi zikulankhula *mwauzimu*. **Iwo sanadetsedwa ndi mipingo ya chipembedzo iyi, iwo ndi anamwali mu uzimu.** Iwo akutsogozedwa aliyense payekha payekha ndi Mzimu wa Mulungu. Kotero tikuona apa kuti

munthu sakuyenera kukhala namwali mu thupi, kuti akakhale namwali mu uzimu. Kotero kuchokera pa maimidwe amenewo, ndi Mulungu yekha amene akudziwa amene ali namwali ndi amene sali, mogwirizana ndi muyeso chake.

Vesi lachisanu likuti, *"Ndipo mkamwa mwao simunapezedwa bodza; ali wopanda chilema."* Kodi zikutanthauza chiyani? Iwo alibe ziphunzitso zina ziri zonse zimene ndizochokera ku seminare kapena kuchokera ku zipembedzo. Iwo amatenga vumbulutso lawo molunjika kuchokera kwa Mulungu ndipo mkamwa mwao simunapezeka bodza, kapena chiphunzitso cha bodza, kapena zamkutu. Iwo ametenga kuchokera kwa Mulungu.

Iwo alibe vuto pamaso pa Mulungu ndipo amatsatira Mwanawankhosa kulikonse kumene apita. Kodi mukuona 144,000 ndi chimene akuyenera kuchita? Iwo sadzalalikira uthenga wa kulapa ndi kulandira Mzimu Woyera. Tsiku limenelo lidzakhala litapita. Inu muli nawo mpata wolapa lero, kubatizidwa mu dzina la Yesu Khristu, ndi kulandira mphatso ya Mzimu Woyera. Inu muli nawo mpata wolowa ndi kukhala gawo la thupi la Khristu, koma posachedwapa tsiku limenelo litha. Mulungu adzasuntha kulowa mu gawo lina la kachitidwe kake.

Mu masukulu ndi makoleji lero, akuphunzitsa zoti kulibe Mulungu. Ndi njira ya m'dierekezi yoyesera kutsuka mitu achinyamata ndi kuyesera kuwapanga iwo kukhulupirira kuti kulibe Mulungu ndipo palibe zoyenera kutsata. Dikirani mpakana 144,000 awa abweremo. Mulungu adzatsegula khomo kwa iwo ndipo Mau a Mulungu adzatuluka. Iwo adzakhala ndi Uthenga kuti alalikire ku dziko lonse, ndipo ndi uthenga otsiriza umene dziko lapansi lidzamva. Mulungu adzapanga njira kwa iwo mu mafuko onse.

Uwu si utumiki usanu wa ku Aefeso 4:11. Utumiki usanu udzatengedwa pamene Mkwatibwi akutengedwa pa dziko. Zikatha izi, dongosolo la Mulungu likupita ku gawo lina losiyana. Likupita mu gawo la aneneri awiri amene tachita nawo mu chaputala cha khumi ndi chimodzi. Zikatha izi, dongosolo la Mulungu likupita mu gawo la 144,000 kulalikira Uthenga Wosatha ndipo iwo akutsatira Mzimu wa Mwanawankhosa kulikonse Iye akuwatsogolera iwo.

Gawo Lachiwiri

Vesi 6: *"Ndipo ndinaona mngelo wina alikuuluka pakati pa mlengalenga, wakukhala nao Uthenga wabwino wosatha, aulalikire kwa iwo akukhala padziko, ndi kwa mtundu uli wonse ndi pfuko ndi manenedwe ndi anthu."*

Dziko lapansi lidzakhala mu chitsitsimutso mu nthawi ya chisautso chachikulu, chifukwa Mulungu adzapanga njira. 144,000 adzalalikira Uthenga ku mafuko onse, mitundu yonse, manenedwe, ndi anthu.

Ayuda atuluka ku Italy, Germany, Russia, U.S.A., ndi maiko ena ambiri. Iwo akhoza kulankhula chilankhulo cha kumene akuchokera ngakhalenso chilankhulo chao cheni cheni chachiyuda. **Pamene akumva za Yesu Khristu kuchokera kwa aneneri awiri, ndi chipembedzo cha bodza, chidzawakumbutsa chimene chinachitika pa tsiku la Pentekosite pamene Ayuda adamva za Yesu kupyolera mwa atumwi. Chifukwa iwo adzakhala atabwerera kumene anali, ndipo mosakhalitsa adzayamba kulalikira ku pfuko limenelo. Momwemonso, pamene 144,000 adzamva aneneri awiri adzabwerera msanga msanga kupita ku dziko lawo kumene adzapita ndi Uthenga Wosatha, ndipo sipadzakhala vuto la chilankhulo kuwatchinga iwo.** Ayuda ndi pfuko lokhalo limene liri lokonzeka kuchita izi mu nthawi yochepa. Taonani chimene Uthenga uwu udzakhale pamene adzayamba kulalikira kuchenjeza dziko lapansi.

Vesi 7: *"Ndikunena ndi mau akulu, opani Mulungu, mpatseni ulemerero pakuti yafika nthawi ya chiweruzo chache, ndipo mlambireni Iye amene adalenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi a kasupe amadzi."*

Uthenga uwu sunalankhulepo chirichonse za kubatizidwa mu dzina la Yesu Khristu. Sunalankhulepo chirichonse za kulapa ndi kulandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pa nthawi imene Uthenga Wosatha ukulalikidwa, tsiku limenelo lidzatha. Mulungu wayamba kuchita mu gawo lina. Kodi iwo adzati chiyani? Opani Mulungu, perekani ulemerero kwa Iye, chifukwa chiweruzo chake chafika.

Mu tsiku iri, chikominisiti changotenga kumene gawo la Kum'mawa Kutali, komanso ena a maiko a ku Ulaya, Canada, ndi U.S.A. akupanga nkhondo. Pali kachitidwe kotsutsa –mulungu ndi zina zotero koma limodzi la masiku amenewa padzabwera uthenga kulimbana nazo zimenezo ndipo ziri mu magawo atatu.

Gawo loyamba ndi kudzutsa anthu ndi kuwalora iwo kudziwa kuti kuli Mulungu. Mulungu adzakhala ndi 144,000 ndi kuwaulura iwo mu njira yapanga uthenga wao kukhala wogwira ntchito. Sakufotokoza chirichonse za iwo kuchiza odwala kapena kuukitsa akufa; koma Mulungu adzatsegula zitseko pamene zitseko zatsekedwa. Mulungu adzapanga njira kuti Mau a Mulungu apite ponseponse. Uthenga Wosatha ndi otsutsana ndi chikominisiti komanso mochuluka Chikatolika. Uthenga uwu umathandizanso kuteteza anthu kuthupi kuzigulitsa okha kwa m'dierekezi ndi ntchito za thupi, kotero kuti Mulungu akakhale ndi anthu a thupi kukadzaza dziko mu mileniamu.

Taonani, iwo amadzutsa anthu ndikuwadziwitsa iwo kuti kuli Mulungu, ndi kuti akuyenera kupembedza Mulungu komanso kuti awope Mulungu.

Kenako gawo lotsatira la Uthenga limene adzalalikira lidzakhala iri:

Vesi 8: *"Ndipo anatsata mngelo wina mnzache ndi kunena, Wagwa, wagwa, Babulo waukulu umene unamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa chigololo chache."*

Choyambirira 144,000 akudzutsa anthu ndikuwadziwitsa kuti kuli Mulungu. Uko ndi kuchiika chikomisiti poyera, mu gawo loyamba la utumiki wao. Gawo lachiwiri likuika chikatolika, chiprotestant, ndi zikhulupiriro zina poyera.

Awa 144,000 amene asindikizidwa Mkwatibwi atapita adzauza dziko lapansi kuti Babulo wagwa. Iwo adzafotokoza m'mene wakhala wovundira mu M'bado wa M'dima. Iwo adzanena za Kuzunza kwa Maspanish ndi m'mene iwo anaikira a Khristu ku imfa ochuluka zikwizikwi. 144,000 awa akudziwa mbiri ya Katolika ndipo iwo adzakhala okwanira **kuliuza** dziko lapansi chimene mai hule ali. Iwo adzati iye wagwa ndipo wapanga mafuko onse kumwa za vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake. Ndi chimene anthu ambiri lero aledzera nacho. Iwo aledzera mwa uzimu. Iwo akumwa vinyo wa chigololo chake. Anthu ambiri amwa kuchokera ku chipembedzo chabodza pa malingaliro a munthu ndi kachitidwe, koma Mkwatibwi wa Yesu Khristu ali ndi Mau.

Vesi 9: *"Ndipo anawatsata mngelo wina, wachitatu, nanena ndi mau akuru, ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lache, nalandira lemba pa mphumi pache, kapena pa dzanja lache."*

Iri ndi gawo lachitatu la utumiki wao. Taonani kusiyana kwa chirombo ndi fano lake; pali chirombo ndipo pali fano. Zotsatira za chimodzi, ndi zoipa ngati chinzake. Ndi koipa kupembedza fano la chirombo, monga kuliri kupembedza chirombo.

Kodi mukudziwa kuti "chilemba cha chirombo" ndi chiyani? Ndi Bungwe la Mipingo pa Dzikolonse ndi zipembedzo zina zonse za zimene zakana Mau. Kodi "chirombo" ndi chiyani? Ndi kachitidwe ka Chiroma, monga mkazi, amene ndi Mpingo wa Katolika ukukwera chirombo cha Chiroma ichi. Chirombo ichi chakhala chiripo kuyambira munyengo ya m'ma B.C., koma osati mkazi amene akuchikwera. Iye anangofika powonekera mu m'bado wachitatu wa mpingo.

Mu chaputala cha khumi ndi chitatu, ife tinabweretsa m'mene fano la chirombo lidzakhalire ndi mphamvu yakulankhula ndikupangitsa kuwapha iwo amene sadzakhala mu mzere. Iye adzakhala ofanana ndi mai wake.

Vesi 10: *"Iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasanganiza m'chikho cha mkwiyo wache; ndipo adzazunzika ndi moto ndi sulfure pamaso pa angelo oyera mtima ndi pamaso pa Mwanawankhosa:"*

Kodi zikutanthauza chiyani pamene akuti *"Vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasanganiza m'chikho cha mkwiyo wache?"* Apo pali chaputala chanu cha khumi ndi chisanu ndi chimodzi cha Bukhu la Chivumbulutso. Miriri idzatsanulidwa ndipo sipadzakhala chifundo.

Vesi 11: *"Ndipo utsi wa kunzunza kwao ukwera ku nthawi za nthawi; ndipo sapuma usana ndi usiku iwo akulambira chilombocho ndi fano lache, ndi iye aliyense akalandira lemba la dzina lache."*

Kodi mukutha kuona chirombo ndi fano lake? China ndi choipa kwambiri ngati chinzake. Ndi chifukwa chake M'bale William Branham anafuula, "Tulukani pakati pawo, anthu anga. Tulukani pakati pawo, iye wathedwa, iye ndi fano!" **Koma tsopano uwo siuthenga wathu woyamba. Uthenga woyamba wa**

Mkwatibwi wa Khristu ndi kulowa mu Thupi la Khristu kuti mukalowe mu Mkwatulo, ndi kukhala mu phwando la ukwati la Mwanawankhosa pamene chaputala ichi chikukwaniritsidwa.

Vesi 12: *"Pano pali chipiriro cha oyera mtima, cha iwo akusunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiriro cha Yesu."*

Apa pali chikhulupiriro cha oyera mtima. Oyera mtima ati? Iwo amene adakana kuyenda mu kachitidwe ka chirombo. Padzakhala oyeramtima ambiri amene adzatsala pamene Mkwatulo uchitika amene alephera kulowa mu Thupi la Khristu. Padzakhala Ayuda apa amene adzaima ndi Mau a Mulungu. *"Pano pali iwo amene asunga malamulo a Mulungu [Ayuda] ndi chikhulupiro cha Yesu [Amitundu]."*

Vesi 13: *"Ndipo ndinamva mau ochokera kumwamba, ndi kunena, Lemba, Odala akufa akumwalira mwa Ambuye, kuyambira tsopano; inde anena Mzimu, kuti apumule ku zolemetsa zao; pakuti ntchito zao zitsatana nao pamodzi."*

"Kuyambira tsopano" zikutanthauza kuti oyeramtima adzafa chifukwa cha kaimidwe kawo pa Mau pamene nthawi iyi iyamba. Taonani izi zikuti, *"Kuti apumule ku zolemetsa zao, pakuti ntchito zao zitsatana nao pamodzi."* Izi zikuonetsera kuti si tsiku ngati limene tikukhalali. Lero si mwa ntchito, koma tafika pansi pa chilungamo cha Mulungu. Chivumbulutso chaputala 18 chikutenga utumiki omwewo wa 144,000 ndikuonetsera kudzoza kwao kwapadera.

Gawo Lachitatu

Tsopano, tikuchita ndi gawo lachitatu. Gawo loyamba lafotokoza za 144,000, chimene iwo ali ndi ntchito yawo. Gawo la chiwiri likuchita ndi Uthenga umene akulalikira. Zonse izi ndi pakati pa sabata.

Gawo lachitatu la chaputala ichi likuchita ndi kukonzekera Nkhondo ya Armageddoni imene iri ku mapeto kwa zaka zitatu ndi theka. Ife tichita ndi izo tsopano kuyambira vesi la khumi ndi chiyani mpakana vesi la makumi awiri.

Vesi 14: *"Ndipo ndinapenya taonani, mtambo woyera; ndi pa mtambo padakhala wina monga Mwana wa munthu, wakukhala naye korona wagolidi pamutu pache, ndi m'dzanja lache zenga lakuthwa."*

Taonani, Yesu anali ndi korona pa mutu Pake ndi zenga mu dzanja Lake kuonetsera kuti walandira kale ulamuliro kuchokera kwa Mulungu Wamphamvu kuti alamulire ngati Mfumu ya mafumu; ameneyo ndiye korona wa golidi wa mutu Wake. Awa ndi maonekedwe auzimu amene Yohane akuwayang'ana. Kachiwiri, Iye ali ndi zenga lakuthwa mu dzanja Lache. Inu ngati muli nalo zenga mu dzanja lanu, ndi lodulira chinachake, sichoncho?

Vesi 15: *"Ndipo mngelo wina anatuluka m'kachisi, wopfuula ndi mau akulu kwa Iye wakukhala pamtambo, tumiza zenga lako ndi kumweta; popeza zinthu za dziko zachetsa."*

Vesi 16: *"Ndipo Iye wokhala pamtambo anaponya zenga lache padziko, ndipo zinthu za dziko zinamwetedwa."*

Izi ndi zochitika zimene zikuchitika Nkhondo ya Armageddoni isanafike. Ndi ulamuliro umene Yesu ali nao kumasula mphamvu zauzimu. Yohane akuona Yesu Khristu pamene Iye akulandira ulamuliro kumasula mphamvu za uzimu kubweretsa pamodzi dziko ku Armageddoni. Iye amangopanga kusesa kwakukulu ndi zenga lakuthwa mu dzanja Lake. Izi zikuchita ndi zochitika zotsogolera ku Nkhondo ya Armageddoni.

Ine ndikufuna kuwerenga kuchokera ku kumasulira kwina ndipo zitithandiza kumvetsa pang'ono. *"Yamba kugwritsa zenga chifukwa nthawi yakwana kuti ukolore, zokolora pa dziko zacha. Kotero iye wokhala mu mtambo anaponya zenga padziko lapansi ndipo zokolora zinatutidwa."* Taonani kuti Iye sakuchita, pa nthawi ino kuwasonkhanitsa palimodzi. Iye akungoponya zenga padziko. Ndi chizindikiro kuchokera kwa Yesu Khristu kwa mphamvu zauzimu zonse; ndipo mphamvu zonse zauzimu zikuyenera kutenga ulamuliro pansi pa Yesu Khristu, kaya mphamvuzo ndi zabwino kapena zoipa, pamene zenga iri liponyedwa pa dziko. Panthawi iyi, mphamvu zonse zauzimu zidzayamba kusuntha dziko lino ku nthawi ya mavuto imene sinakhalepo dziko lapansi lisanakhale. Muone kuti Iye sanadule dziko lapansi; Iye anangoponyera pa dziko lapansi. Mwa kulankhula kwina, masulani mphamvu za uzimu zimene zidzasonkhanitsa dziko lapansi pamodzi ndikubweretsa Armageddoni. Izi zikuonetsera chinthu

chomwecho ngati angelo anai omangidwa mu mtsinje wa Firate pansi pa lipenga la chisanu ndi chimodzi kumene akuti "masulani angelo anai omangidwa mu mtsinje wa Firate." Chinthu chomwechi chaonetseredwa mu muliri wa chisanu ndi chimodzi pamene mizimu yodetsedwa itatu ngati achule ikutuluka pakamwa pa chinjoka, pakamwa pa chirombo, ndi pakamwa pa aneneri abodza, kusonkhanitsa dziko lapansi ku Armageddoni. Ndi Yesu Khristu ndi ulamuliro wa Mulungu Mkwatulo utachitika, Iye atatha kulandira ulamuliro wake wachifumu, Iye atatha kulandira mphamvu kudzaweruza dziko lapansi, Iye adamasula mphamvu zina zauzimu mu dziko ndipo dziko lonse lapansi linayamba kuchita ndi Ulamuliro wache.

Vesi 17: *"Ndipo mngelo wina anatuluka m'kachisi ali m'Mwamba, nakhala nalo zenga lakuthwa nayenso."*

Vesi 18: *"Ndipo mngelo wina anatuluka pa guwa la nsembe, ndiye wakukhala nao ulamuliro pamoto; napfuula ndi mau akuru kwa iye wakukhala nalo zenga lakuthwa, nanena, Tumiza zenga lako lakuthwa, nudule matsango a munda wampesa wa m'dziko; pakuti mphesa zake zapsa ndithu."*

Kumasulira kwina kukuti, *"Gwiritsa ntchito zenga lako kudula ziatso zonse ku mpesa wa pa dziko lapansi chifukwa wakwanira pa chiweruzo."*

Vesi 19: *"Ndipo mngelo anaponya zenga lache ku dziko nadula mphesa za m'munda wa dziko, naziponya moponderamo mphesa mwamukuru mwa mkwiyo wa Mulungu."*

Vesi 20: *"Ndipo moponderamo mphesa anamuponda kunja kwa mudzi, ndipo mudatuluka mwazi moponderamo mphesa, kufikira zapakamwa za akavalo, kufikira mastadiya chikwi ndi mazana asanu ndi limodzi."*

Kutanthauzira kwina kukuti, *"Ndipo mpesa unapondedwa moponderamo mpesa kunja kwa mzinda, ndipo mwazi unatsika kuchokera mu mitsinje mamailosi mazana awiri kutalika, kutalika kufikira zapakamwa za a kavalo."* Kumeneko ndi kuchigwa cha Megiddo.

Yesu, akukhala pamenepo mumasomphenya, anaponya zenga pa dziko. Chinali chizindikiro kwa mphamvu zonse za uzimu kuti "pitani mukachite chirichonse mukufuna kuchita." Kenako mngelo anatenga ntchito kuti awone chimene Mau a Mulungu akukwaniritsa.

Dziko iri liri mu chivundi lero. Palibe chochita, koma kulononga basi. **Mtundu wa anthu, matupi, afika pa chivundi moti zimangotengera kudziwidwiratu ndi Mzimu wa Mulungu kubwera ndi kusintha izo. Munthu wafika poyipa kuposa chinyama. Pamene Mulungu ayang'ana pansi, Iye amaona kuti zafika pakucha kwathunthu. Dziko ndi chivundi chachikulu. Kodi Iye amatani? Iye amawasonkhanitsa iwo mu Chigwa cha Magiddo ndipo Mulungu amadzuka ndi kumayendayenda pa icho ndikumaponda iwo mpakana mwazi utatuluka ma mailosi mazana awiri mpakana zapakamwa za a kavalo.** Apa ine ndikulankhula mwazoimirira.

Ndi m'mene Yohane anazionera. Iwo sadzakwera a kavalo pa nkhondoyo, koma izi zikuonetsera chionongeko chachikulu. Mamilioni adzafa uko ku Nkhondo ya Armageddoni 144,000 atangotha kulalika uthenga wao. Inu mukhoza kupita ku Chivumbulutso chaputala 19, kumene akuponda mopondera mpesa wa mkwiyo wa Mulungu. Komanso, Chivumbulutso 19 chikugwirizana ndi ichi. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHAKHUMI NDI CHISANU

Vesi 1: *"Ndipo ndinaona chizindikiro china mwamba, chachikulu ndi chozwizitsa, angelo asanu ndi awiri akukhala nayo miriri isanu ndi iwiri, ndiyo yotsiriza, kuti mwa iyo watsirizika mkwiyo wa Mulungu."*

Mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chimodzi tichita ndi miriri isanu ndi iwiri. Imodzi mwa miriri isanatsanulidwe, Mulungu asanayambe kutsanulira chiweruzo Chake, muliri umodzi pa unzake zifika pa dziko. Kachisi ali ndi utsi ndipo palibe amene akhoza kulowamo. Pali mabingu ndi mphenzi zikuchitika mu kachisi, ndipo pali chiweruzo pa dziko, koma pa nyanja ya mandala pali iwo amene anapereka miyoyo yawo mu nthawi ya chisautso chachikulu pa chifukwa cha Mulungu.

Vesi 2: *"Ndipo ndinaona ngati nyanja ya mandala yosanganiza ndi moto; ndipo iwo amene anachilaka chirombocho, ndi fano lache ndi chiwerengero cha dzina lache, anaimirira pa nyanja ya mandala, nakhala nao azeze a Mulungu."*

Nyanja iyi ya mandala ndiyosakaniza ndi moto. Kodi moto uwu ndi chiyani? Ndi moto wa chisautso. Awa ndi maonekedwe a kumwamba. Yohane adaona miyoyo ya iwo amene adaphedwa ndi chirombo ndi aneneri onama mu chisautso chachikulu ndipo akuima pa mpando wa chifumu wa Mulungu. Yohane anawaona iwo ataima pa nyanja ya mandala. **Taonani kuti iwo amene akuima pa nyanja ya mandala agonjetsa chirombo, fano la chirombo, ndipo nambala ikuonetsa kuti iwo ndi oyeramtima aku chisautso, chifukwa ndi pamene chirombo ndi fano lake chikulankhula; kotero awa akuyenera kukhala oyeramtima aku chisautso.**

Izi zikhoza kuoneka ngati zotsutsana kwa lingaliro la thupi pamene tikuona ku chaputala cha khumi ndi chitatu cha Chivumbulutso, kumene akuti kunapatsidwa kwa chirombo kuchita nkhondo ndi oyeramtima ndi kuwagonjetsa iwo. Ngati oyeramtima anagonjetsedwa, nanga iwo anapeza bwanji chigonjetso? Chirombo chinawagonjetsa *mwathupi.* Chivumbulutso 14:13 akuti, *"Odala ali akufa amene amwalira mwa Ambuye."* Kotero, iwo anapeza chigonjetso mwa kuima mokhulupirika ndi kuphedwa chifukwa cha Mau a Mulungu ndi kugonjetsa chirombo mwa *uzimu.* Chirombo chinawagonjetsa iwo mwathupi, koma iwo anapeza chigonjetso. Zikanatha kuoneka ngati iwo amaluza, koma amapambana ndi kugonjetsa chifukwa iwo anapereka miyoyo chifukwa cha maimidwe awo pa Mau mu nyengo ya chisautso. Ichi ndi chithunzi cha miyoyo imene inaphedwa chifukwa cha Mau a Mulungu ndi chifukwa cha umboni wa Khristu.

Vesi 3: *"Ndipo ayimba nyimbo ya Mose kapolo wa Mulungu, ndi nyimbo ya Mwanawankhosa, nanena, Ntchito zanu ndi zazikulu ndi zozizwitsa, Ambuye Mulungu, Wamphamvuyonse; njira zanu nzolungama ndi zoona, Mfumu Inu ya oyeramtima."*

Iwo anaimba nyimbo ya Mose, kapolo wa Mulungu, ndi nyimbo ya Mwanawankhosa. Iwo anati, *"Ntchito zanu ndi zazikulu ndi zozwizwitsa, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse."* Kodi Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse ndani? Ayuda amakhulupirira mwa Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse. Mulungu anali ndi Yohane kumulembera izi kuti azipange momveka kulekanitsa pakati pa Ayuda ndi Amitundu. Lotsatira la vesi iri likuti, *"Njira zanu nzolungama ndi zoona, Ambuye, Mulungu Wamphamvuzonse."* Kwa Amitundu, Yesu Khristu ndi Mfumu ya oyeramtima.

Onse a iwo akuima pa nyanja ya mandala, onse Ayuda ndi Amitundu adzadziwa kuti Yesu ndiye Khristu. Ngakhale kuti panali a Ayuda ambiri amene sanadziwe pamene anafa chifukwa cha Mau a Mulungu, iwo adzadziwa izo pamene adzaima pa nyanja ya mandala. Mulungu adamulora Yohane kuziona izo mu njira iyi kuti tikathe kumasulira Mau mu tsiku iri lotsiriza ndikudziwa kuti ndi onse Ayuda ndi Amitundu. Iwo ali kutamanda Mulungu ndi kuimba nyimbo ya Mose ndi ya Mwanawankhosa.

Vesi 4: *"Ndani adzakhala wosaopa ndi kulemekeza dzina lanu Ambuye? Chifukwa inu nokha muli woyera; chifukwa mitundu yonse idzadza nidzalambira pamaso panu, popeza zolungama zanu zidaonetseredwa."*

Ine ndikufuna ndikufunseni inu funso, ndipo funsolo pa lokha litanthauzira yankho. Kodi iwo angatenge kuti mau monga, *"Ndani adzakhala osaopa Inu?"* Ganizirani za chaputala cha khumi ndi chinai ndipo ndikuonetserani inu. Kodi uthenga wa 144,000 unali chiyani? *"Opani Mulungu, ndipo perekani ulemerero kwa Iye; chifukwa ora ya chiweruzo chake lafika."* Awa amene akuima pa nyanja ya mandala anali okhudzidwa ndi uthenga wa 144,000. **Awa 144,000 anali zida zolimbikitsa iwo kuti amwalire chifukwa cha chikhulupiriro chimene anali nacho mwa Mulungu.** Kodi mukuona m'mene Mau a Mulungu alembedwera? Kodi sizokoma? Akanati 144,000 asapitirire ndi kulalikira uthenga wa mtundu umenewo, pafupifupi dziko lonse likanadzalambira chirombo.

Vesi 5: *"Ndipo zitatha izi ndinaona, ndipo panatseguka pa kachisi wa chihema cha umboni m'Mwamba."*

Izi zikuonetsa kumapeto kwa chiombolo pansi pa gawo lotsiriza iri. Kumasulira kwina kwa vesi iri kukuti, *"Zitatha izi ndinapenya ndipo kachisi anatsegulidwa konse mpakana ku malo oyeretetsa."* Kodi zikutanthauza chiyani? Palibenso chiombolo cha maonekedwe amenewo pa dziko pano.

Pa nthawi iyi, Uthenga umene 144,000 analalikira wafika kumapeto. Unali ndi chochita pa dziko ndipo dziko lasambisidwa mu mwazi; ndipo Yohane adaona miyoyo pa nyanja ya mandala.
Vesi 6: *"Ndipo anatuluka m'Kachisi angelo asanu ndi awiri akukhala nayo miriri isanu ndi iwiri, atavala mwala woyera, ndi wonyezemira, namangira malamba agolidi pachifuwa pawo."*
Vesi 7: *"Ndipo chimodzi cha zamoyo zinai chinapatsa angelo asanu ndi awiri mbale zisanu ndi ziwiri zagolidi zodzala ndi mkwiyo wa Mulungu wakukhala ndi moyo ku nthawi za nthawi."*

Pa mfundo yakuti angelo asanu ndi awiri awa apatsidwa miriri isanu ndi iwiri, zikutanthauza kuti iwo atsiriza kale pamodzi ndi mabingu asanu ndi awiri. Angelo amene ali ndi malipenga ndi angelo amene apatsidwa miriri ndi angelo omwewo asanu ndi awiri.

Vesi 8: *"Ndipo kachisi anadzadzidwa ndi utsi wochokera ku ulemelero wa Mulungu ndi ku mphamvu yache; ndipo palibe munthu anakhoza kulowa m'Kachisi kufikira ikatha miriri isanu ndi iwiri ya angelo asanu ndi awiri."*

Taonani ulemerero wa Mulungu ukubwera mu kachisi. Ulemerero uwu si ulemerero mu chifundo, koma ndi ulemerero wa Mulungu mu chiweruzo. Mulungu ndi wa ulemerero mu chifundo. Mulungu ndi wa ulemerero mu chiweruzo Chake. Mulungu ndi wa chilungamo mu chifundo Chake, ndipo Mulungu ndi wachilungamo mu chiweruzo Chake. Akunena mu vesi 4 kuti, *"Chiweruzo chanu chaonekera."* Mulungu akuyamba kuweruza ndi kutsanulira mkwiyo Wake. Palibe munthu amene anathanso kulowa mu kachisi, kutanthauza kuti panalibenso china chirichonse chochitika kuthandizira mtundu wa anthu. Zinali zitafika kumapeto. Chinali chiweruzo cha Mulungu. Panalibe mwazi [choimirira] pa mpando wa chifundo, kotero palibenso chifundo.

Ine ndikufuna ndiwerenge lemba limodzi ndikukuonetserani inu chimene chiri pamaso pa Mulungu popanda chifundo ndi kusalandira msembe pa Likasa la Pangano. 1 Samueli 6:19- *"Ndipo Mulungu anakantha anthu a ku Betisemesi, chifukwa anasuzumira mu likasa la Yehova, anakantha anthu zikwi makumi asanu; ndipo anthu analira maliro, chifukwa Yehova anawakantha anthuwo ndi makanthidwe akulu."* Chinali chiyani? Anthu anabweretsedwa ku lamulo la Mulungu popanda mwazi pakati pa iwo ndi Mulungu. Pamene iwo anachotsa chovindikira cha pa likasa [choovindikira chinali mpando wa chifundo] chimenecho chinatenga mpando wa chifundo kuchokera ku lamulo la Mulungu ndi anthu. Kodi mukuziona izo tsopano? Chinachitika ndi chiyani? Mkwiyo wa Mulungu unawatulukira iwo ndipo unapha anthu 50,070, kuonetsera chimene mkwiyo wa Mulungu uli. Ichi chikuchita ndi chinthu chomwecho pamene Likasa la Pangano linali. Chikuonetsera chiweruzo cha Mulungu.

Kodi mukumuona Mulungu wa mkwiyo wa ku Chipangano Chakale akubwera poyera kachiwirinso? Mulungu wa mkwiyo, Mulungu wa ku Chipangano Chakale, Mulungu amene ife sitinamuonepo akusuntha mu mkwiyo, akubweranso poyera. Palibe ngakhale muliri umodzi umene ungatsanulidwe mpakana kachisi kumwamba atatsegulidwa, mpakana Likasa la Pangano litabweretsedwa poyera, chifukwa zimaonetsera kuti pali chifundo cha mtundu wina. Mtundu wa chifundo umene amalandira si ngati umene tiri nawo tsopano, koma pansi pa 144,000 Mulungu anapanga njira ku utumiki wao; ndipo Mulungu anapanga njira kwa anthu kuti awamvere iwo. Mulungu anapereka chisomo kwa iwo akumuopa Iye, kupereka ulemu ku dzina lake, ndi kuima ndi Mau a munthawi imeneyo, koma apa kachisi akutsegulidwa ndipo chifundo chonse chatha. Mulungu akukonzekera kutseka m'bado ndi kuweruza. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHISANU NDI CHIMODZI

Vesi 1: *"Ndipo ndinamva mau akulu ochokera ku Kachisi, akunena kwa angelo asanu ndi awiri, Mukani, ndipo tsanulirani kudziko mbale zisanu ndi ziwiri za mkwiyo wa Mulungu."*

Taonani kuti mau akulu anatuluka mu kachisi. **Awa simau a Yesu, wokhala pakati apa.** Awa ndi mau a Yehova, mzimu wamuyaya, kunena, "Pitani njira zanu." Chonse chimene chikuoneka ndi utsi kuchokera ku ulemerero wa Mulungu, ndipo angelo asanu ndi awiri anabwera. Palibe aliyense amene akanatha kuwaletsa angelo awa. Palibe mwazi pa mpando wa chifundo, ngakhale chifundo. Ine ndikulankhula mwa zoimirira; pakhala palibe mwazi weniweni kumwamba.

Vesi 2: *"Ndipo anachoka woyamba, natsanulira mbale yache kudziko; ndipo kunakhala chironda choipa ndi chosautsa pa anthu akukhala nalo lemba la chirombo nalambira fano lache."*

Pamene miriri itsanulidwa, siikutsanulidwira pa anthu kuwaweruza iwo ndikuyesera kuwapanga iwo kuti alape. Iyo ikutsanulidwa kwa anthu ngati mkwiyo wolunjika kuchokera kwa Mulungu. Izo ndi chinthu chosiyana ndi mabingu pamene ayamba kuomba. Icho chidzakhala chiweruzo cha Mulungu kuyesera kudzutsa mafuko a Israeli, kuwatengera iwo kuona chimene zawatengera posainira pangano ndi papa.

Pamene lipenga loyamba liomba ..., matalala, moto, ndi mwazi zinagwa pa dziko, kodi mukudziwa kuti zinagwa pa chiyani? Zinagwa pa msipu wobiriwira ndi mitengo yobiriwira. Tiyeni tiwerenge zimenezo mu chaputala cha chisanu ndi chitatu ndi kukuonetserani m'mene mabingu asanu ndi awiri akuyendera limodzi ndi miriri isanu ndi iwiri. Chivumbulutso 8:6-7 – *"Ndipo angelo asanu ndi awiri akukhala nawo malipenga anadzikonzera kuti aombe. Ndipo woyamba anaomba, ndipo padakhala matalala ndi moto, zosanganiza ndi mwazi, ndipo anazitaya pa dziko lapansi; ndipo limodzi la magawo atatu a dziko lidapserera, ndipo msipu wonse udapserera."* Pamene lipenga iri liomba mkwiyo wa Mulungu siugwa pa anthu, ugwa pa mitengo ndi msipu. Adzakhala Mulungu kuyesera kudzutsa Israeli, **koma pamene muliri woyamba utsanuridwa sukhala pa msipu kapena mitengo. Ndi kwa mtundu wa anthu wochimwa.** Ndi mkwiyo wa Mulungu, chiweruzo cha Mulungu, chikutsanulidwa pa anthu amene apembedza kale chirombo, amene atenga kale chilemba cha chirombo, ndipo amene apembedza kale fano. Pamene muliri woyamba utsanuridwa unayambitsa zilonda zazikulu pa iwo amene akana Mulungu mu njira Yake.

Pamene malipenga woyambirira anai akuomba palibe chirombo choti chipembedzedwe, kotero kuti, chikungofika ku kupangidwa. Chirombo chidzangofuna kupembedzedwa pakati pa sabata. Muliri woyamba uwu uli kuyandikira kumapeto kwa sabata. Iyi ndi nthawi ya Mulungu ya kutsanulira chiweruzo pa anthu amenewo amene akana ndi kuchikana chifundo cha Mulungu**. Miriri iyi ikutsanulidwa pafupifupi zaka zisanu ndi ziwiri lipenga loyamba litaomba, ngakhale kachitidwe kake ndi komanga zonse kudutsa mu zaka zitatu ndi theka za sabata.** Izi zaonetsedwa ndi muliri wa chisanu komanso wachisanu ndi chimodzi mudzaona pamene tichita ndi izo kutsogolo mu chaputala ichi.

Vesi 3: *"Ndipo mngelo wachiwiri anatsanulira mbale yache m'nyanja; ndipo kunakhala mwazi ngati wa munthu wakufa; ndipo zamoyo zonse za m'nyanja zidafa."*

Ichi ndi chinthu cha dziko lonse. Mulungu akuweruza dziko lino lapansi. Tiyeni tione ku lipenga lachiwiri ndi kukuonetserani kuti latsanulidwa pa gawo limodzi la magawo atatu a nyanja. Chivumbulutso 8:8-9- *"Ndipo Mngelo wachiwiri anaomba, ndipo monga ngati phiri lalikulu lakupserera ndi moto linaponyedwa m'nyanja, ndipo limodzi la magawo atatu a nyanja linasanduka mwazi; ndipo lidagwa limodzi la magawo atatu a zolengedwa ziri m'nyanja, zokhala ndi moyo, ndipo limodzi la magawo atatu a zombo lidaonongeka."*

Pamene lipenga lachiwiri liomba, lidzakhala likuchita ndi Israeli. Ndi mzimu wa Mose pa m'neneri kusandutsa nyanja ya Mediterrane kukhala mwazi, koma pamene mnngelo wachiwiri atsanulira muliri wake pa nyanja ikusanduka Mwazi. Ndi chiweruzo cha Mulungu, ndipo sizikuchitika ku dera lirilonse. Pa nthawi iyi dziko lonse la uneneri lalambira chirombo ndi fano lache. Kotero Mulungu akuyamba kutsanulira miriri yake. Mwa kulankhula kwina, Iye akuonjezera muyezo wina wa gasoline pa moto.

Pamene miriri isanu ndi iwiri imeneyi itsanulidwa anthu onse sadzafa koma Mulungu sadzaika kwa izo ku dera lirilonse monga Iye anachitira pamene malipenga oyamba ochepa aomba. Apa, Iye akutsanulira chiweruzo pa dziko lonse la uneneri.

Taonani kuti lipenga lachiwiri likuyenera kuchita ndi nyanja kusandulika magazi. Koma lipenga likungosandutsa gawo lachitatu kukhala mwazi. Muliri wachiwiri ulibe malire; ndi chimene Mulungu akuchifuna.

Vesi 4: *"Ndipo mngelo wachitatu anatsanulira mbale yache ku mitsinje ndi akasupe a madzi; ndipo kunasanduka mwazi."*

Vesi 5: *"Ndipo ndinamva mngelo wa madziwo nanena, Muli wolungama, amene muli, nimunali, Woyera Inu, chifukwa mudaweruza kotero."*

Vesi 6: *"Popeza anatsanulira mwazi wa oyeramtima, ndi wa aneneri, ndipo mudawapatsa mwazi amwe; ayenera iwo."*

Vesi 7: *"Ndipo ndinamva wa pa guwa la msembe alikunena, Inde, Ambuye Mulungu, Wamphamvuzonse, maweruziro anu ali woona ndi olungama."*

Apa pali chiweruzo chikutsanulidwa ndi Ambuye Mulungu wa mphamvuzonse. **Ndi Ambuye wamphamvuzonse wa ku Chipangano Chakale kutsanulira chiweruzo Chake, kusintha mitsinje ya madzi ya dziko lapansi kukhala mwazi, ndi anthu kufa ndi miriri. Sikuti ndi mitsinje yonse. Mulungu akudziwa m'mene angasungire anthu amene mwa iwo muli zoyenera,** koma palibe wina apa woti ayende pakati pa Mulungu ndi chiweruzo, kotero Iye amayamba kutsanula mkwiyo Wake.

Tiyeni tifananitse lipenga la chitatu ndi muliri wa chitatu. Muliri wachitatu ukuchita ndi mitsinje ya madzi iyo kusandulika mwazi. Lipenga lachitatu likuchita ndi gawo lachitatu, kuchita ndi Israeli. Chivumbulutso 8:10-11- *"Ndipo anaomba mngelo wachiatatu, ndipo idagwa kuchokera kumwamba nyenyezi yaikulu, yoyaka ngati muuni, ndipo igawa pa limodzi la magawo atatu a mitsinje, ndi pa akasupe a madzi; ndipo dzina lache la nyenyeziyo alitcha Chowawa; ndipo limodzi la magawo atatu a madzi lidasanduka chowawa; ndipo anthu ambiri adafa pakumwa madzi pakuti anasanduka owawa."* **Lipenga iri ndi chiweruzo chochepa.** Pakadali chifundo pamene Mulungu ayamba kuchita mu malipenga ndipo zikungokhudza gawo limodzi la magawo atatu, **koma pamene miriri itsanulidwa palibe malire pa iwo.** Ndi mkwiyo wa Mulungu kutsanuridwa mopanda chifundo.

Vesi 8: *"Ndipo mngelo wachinai anatsanulira mbale yache padzuwa; ndipo analipatsa ilo litenthe anthu ndi moto."*

Vesi 9: *"Ndipo anatenthedwa anthu ndi kutentha kwakulu; ndipo anachitira mwano dzina la Mulungu wokhala nao ulamuliro pa miriri iyi; ndipo sanalapa kuti anchitire ulemu."*

Taonani gawo lotsiriza la izi. Likuti, *"Ndipo sanalapa kuti anchitire ulemu."* Ndi mwai kulapa. Ndi mwai waukulu umene Mulungu wapereka ku mtundu wa anthu kuti afike ku malo kumene akhoza kuzindikira kuti chifundo cha Mulungu chikuchita nawo ndipo akhoza kulapa ndi kutchula pa dzina la Mulungu. Koma apa, mwai umenewo wachotsedwa. Palibe malo opezeka mwa iwo kuti alape.

Muliri wa chinai watsanulidwa pa dzuwa. Chirichonse chimene Mulungu akuchita ku dzuwa pa nthawi ya muliri wa chinai chidzapangitsa kuipitsa anthu ndipo iwo adzachitira mwano Mulungu, ndipo sadzalapa ndi kuitanira pa Mulungu amene ali ndi mphamvu pa miriri iyi.

Tiyeni tifananitse chaputala cha chinai ndi muliri wachinai. Chivumbulutso 8:12- *"Ndipo mngelo wachinai anaomba, ndipo limodzi la magawo atatu a dzuwa linagwidwa, ndi limodzi la magawo atatu a mwezi, ndi limodzi la magawo atatu a nyenyezi; kuti limodzi la magawo awo atatu lidetsedwe, ndi kuti limodzi la magawo ache atatu a usana lisawale, ndi usiku momwemo."*

Pamene lipenga lachinai likuomba, likuchita ndi dzuwa. Ndi Mulungu kuzimitsa nyali zonse kuyesera kudzutsa Israeli. Ndi chenjezo. Koma pamene miriri wa chinai utsanulidwa, Iye akuutsanulira pa dzuwa ndi kupanga iwo kudetsa anthu pamene akukhala pa dziko lino. Mulungu akulanga mtundu wa anthu akugwa, ndipo izi zichitika mu m'bado uno.

Vesi 10: *"Ndipo mngelo wachisanu anatsanulira mbale yache pa mpando wa chifumu wa chirombo; ndipo ufumu wache unadetsedwa; ndipo anatafuna malirime ao ndi kuwawa kwache."*

Vesi 11: *"Nachitira mwano Mulungu wa m'Mwamba chifukwa cha zowawa zawo ndi zironda zawo; ndipo sanalapa ntchito zao."*

Kodi zironda anazitenga kuti? Kodi kuwawa uku anakutenga kuti? Ndi zotsatira za mngelo woyamba kutsanulira muliri wache. Mu vesi lachiwiri, pamene mngelo woyamba anatsanulira muliri wache pa anthu amene anakana Mulungu, panali zironda zoopsa ndi miriri imene inagwa pa iwo, ndipo adakali nazo pamene mngelo wachisanu akutsanulira muliri wache.

Angelo awa akutsanulira mbale izi zodzala ndi mkwiyo pafupipafupi. Wachisanu ukutsanulidwa pa mpando wa chirombo ndipo ufumu wake ukusandulika wodzala ndi m'dima. **Kodi mpando wa chirombo uli kuti? Ndi Vatican**. Ngakhale kuti papa iyemwini adzasamukira ku Yerusalemu, ntchito zonse zidzidzachitikira ku Roma. Mzinda wa Vatican ndi malo akulu. Ndi amodzi mwa malo a za chuma pa dziko lonse. Ntchito zikupitirira; ndipo zonse za zimenezo sizidzasamukira ku kachisi wa Chiyuda amene adzamangidwanso mu tsiku lotsirizali. Ofesi yokha yakeyake ya papa isunthidwa kupita ku Yerusalemu.

Kodi zikutanthauza chiyani pamene ufumu wake ukusandulika wodzala ndi m'dima? Papa adzapambana kupyolera mwa kachitidwe ka chirombo kubweretsa dongosolo la dziko lonse. Zidzaoneka zabwino kwa munthu wathupi ndipo adzakhala ndi muyeso wa dongosolo, koma pamene Mulungu ayamba kutsanulira chiweruzo Chake mngelo wa chisanu adzatsanulira muliri wake pa zinthu zimene papa akuganizira kuti akuzilamulira. Kenako, mwadzidzidzi adzasiya kumumvera papa. Palibe dongosolo, ndi chisokonezo. Mulungu akuchotsa mphamvu zonse ndipo mpingo wa Chiroma ukulowa mu chisokonezo. Muliri watsanulidwa penipeni pa mpando wa papa ndipo ufumu wake ukusandulika wodzala ndi m'dima. Mulungu akukonzekera kuweruza. Mulungu akukonzekera tsopano kuwononga Mpingo wa Katolika wa Chiroma ndi fano la chirombo.

Tiyeni tione ku lipenga lachisanu. Chivumbulutso 9:1-2- *"Ndipo mngelo wachisanu anaomba, ndipo ndinaona nyenyezi yochokera kumwamba idagwa padziko; ndipo anampatsa iye chifungulo cha dzenje la phompho. Ndipo anatsegula pa dzenje la phompho; ndipo unakwera utsi wotuluka m'dzenjemo, ngati utsi wa ng'anjo yaikulu; ndipo dzuwa ndi thambo zidada, chifukwa cha utsiwo wa kudzenje."*

Lipenga la chisanu liri pakati pa sabata ndipo likulora ziwanda kumasulidwa kuti zigwire ntchito mu kachitidwe ka chirombo mpakana Mulungu atakonzeka kuweruza icho. Pansi pa lipenga lachisanu panali m'dima, ndipo pansi pa muliri wa chisanu pali m'dima. Muliri wachisanu ndi wachisanu ndi chiwiri ndi chimene lipenga lachisanu ndi lipenga lachisanu ndi chiwiri linabereka. Mpingo wa Katolika wataya mphamvu ndi kutaya ulamuliro wake.

Mu nthawi iyi, kutairira kwayamba pa dziko lonse lapansi. Pamene izi ziyamba kuchitika atsogoleri a chikominisiti, nyanga khumi, akuona kuti chinachake sichikuyenda bwino. Iwo akudziwa kuti chinthu chimene anthu akhala akuchikhulupirira, chinthu chimene akhala akuchithandizira chayamba kugwa. Iwo akuona kuti dongosolo la dziko limene linaikidwa siirinso pamodzi. Likuyamba kubwera ku kusalumikizana. Iwo akuyamba kunena, "Iyi ndi nthawi yathu." Nthawi yomweyo Mulungu akuika mu mitima ya mafuko khumiwo kuti awononge Vatican. Mulungu adzaika mu mtima mwao kukwaniritsa cholinga Chake. [Chivumbulutso 17:16-18]

Vesi 12: *"Ndipo wa chisanu ndi chimodzi anatsanulira mbale yache pa mtsinje waukulu Firate; ndi madzi ache anaphwa, kuti ikonzeke njira ya mafumu ochokera patuluka dzuwa."*

Vesi 13: *"Ndipo ndinaona motuluka m'kamwa mwa chinjoka ndi m' kamwa mwa chirombo, ndi m'kamwa mwa mneneri wonyenga mizimu itatu yonyansa, ngati a chule."*

Vesi 14: *"Pakuti ali mizimu ya ziwanda zakuchita zizindikiro; zimene zituruka kunka kwa mafumu a dziko lonse, kuwasonkhanitsira ku nkhondo ya tsiku lalikuru la Mulungu, Wamphamvuyonse."*

Chinjoka ndi mdierekezi mwiniwake. Chirombo ndi kulumikazana kwa kachitidwe ka chirombo kamene ali nako pano pa dziko lapansi. Uku ndi kupitiriza kwa muliri wa chisanu. Mizimu imene inaikidwa ku malo ena kuti ichite ntchito ina yake yamasulidwa. Taonani kuti akuti "chinjoka." Ndi mdierekezi mwiniwake. Chirombo ndi kachitidwe ka nyanga khumi za ku Ulaya. Mneneri wa bodza ndi papa. Izi zikuimirira kachitidwe konseko, ndipo zikutanthauza kuti zikutuluka kunja. Chirombo chimene papa akulamulira sichikumutetezeranso, koma chikuima pa chokha.

Ngakhale satana wataya mphamvu [kupyolera mwa papa] pa zolinga zake, pamene Mulungu ayamba kukwaniritsa Mau Ake. Apo pali mizimu yanu yodetsedwa ngati achule.

Awa ndi masomphenya amene Yohane adawaona, koma njira yabwino kwambiri kuona ziwanda zikutuluka kuchokera pakamwa pa chinjoka, chirombo, ndi aneneri onama, kusiyana ndi achule woonda. Vesi 14 likuti ndi mizimu ya adierekezi. Yohane sakanatha kuona mizimu, koma achule amenewa akuimirira mizimu. Izi zikuonetsera kugwa kwa ulamuliro wa chirombo pamene ziwanda izi zikupita Kum'mawa Kutali ndi kuchita zodabwitsa. Pamene zikusiya kachitidwe ka chirombo ndi kupita Kum'mawa Kutali, iwo adzagwirizana pamodzi Kum'mawa Kutali kubweretsa nkhondo ya Armageddoni.

Ziwanda izi zikupita kuchita zodabwitsa. Zozizwa izi sikuchiritsa matenda kapena kuukitsa akufa. Izi ndi zozizwa za ndale. Zikhoza kungotengera chozizwa cha ndale pakali pano kuti mubweretse pamodzi Kum'mawa Kutali, koma ziwanda izi zidzachita ntchitoyo.

Tiyeni tione kuomba kwa lipenga lachisanu ndi chimodzi ndi kukuonetserani kuti ikubweretsa dziko lonse ku nkhondo. Likuyika Kum'mawa Kutali mu chimodzimodzi. Chivumbulutso 9:13-15- *"Ndipo mngelo wachisanu ndi chimodzi anaomba, ndipo ndinamva mau ochokera ku nyanga za guwa la nsembe lagolidi liri pamaso pa Mulungu. Nanena kwa mngelo wachisanu ndi chimodzi wakukhala ndi lipenga, Masula angelo anai omangidwa pa mtsinje waukuru Firate. Ndipo anamasulidwa angelo anai, okonzera kufikira ora ndi tsiku la mwezi ndi chaka, kuti akaphe limodzi la magawo atatu a anthu."*

Taonani mtsinje wa Firate. Ukutchulidwa mu kuomba kwa lipenga la chisanu ndi chimodzi ndi kutsanulidwa kwa muliri wa chisanu ndi chimodzi. Mu nthawi yakale, mtsinje wa Firate umakhala ngati chotchinga chachilengedwe pakati pa Kum'mawa Pakati ndi Kum'mawa Kutali. Panali nthawi zina pa chaka zimene ankhondo amakhoza kudutsa chifukwa panali mchenga ndiye amatha kulowa, koma tikudziwa kuti palibe mtsinje wa chilengedwe umene ungalepheretse ankhondo mu tsiku iri la mayendedwe amakono. Kotero kuti kuphwa kwa mtsinje ndi chongoimirira chabe. Ndi Mulungu kuchotsa ndi kuimika mphamvu kuchokera kwa mafumu a Kum'mawa amene samagwirizana ndi kachitidwe ka chirombo cha Kumadzulo kwa Ulaya. Kutali Kum'mawa ndi ma Orientals iwo sadzakhudzidwa kwambiri ndi kachitidwe ka chirombo chimene chikulamulira ku Ulaya; kapena kukakamizidwa kutenga chilemba cha chirombo kapena kupembedza fano lache. Iwo sadzatero, ndipo sanayambe atero, kukhala gawo la dziko la uneneri. *"Mafumu a Kum'mawa"* ali ndi chawochawo chikoministi ndipo sichingakhale mu boma la demokalase ngati chikominisiti cha ku Ulaya chingachitire.

Lero pali mitundu iwiri ikulu ikulu ya chikominisiti. Choyamba, pali mtundu wa ku Russia. Kachiwiri pali mtundu wa ma Orientals kapena Kutali ku M'mawa. Kachitatu, pali mtundu watsopano, ndipo ukutchedwa Komunisti wa Ulaya, ndipo uli kwenikweni ku Ulaya. Mitundu itatu imeneyi ikufika kumapeto mu dongosolo la m'mene lalembedwera apa. Mtundu wa Russia ukufika ku mapeto pamene Russia akugonjetsedwa ku dziko la Israeli. Ezekieli chaputala 38 ndi 39 akuonetsa mtundu umenewu wa chikoministiukuwonongedwa pamene Mulungu akumenyera Israeli lisanafike sabata la 70 la Danieli ku chiyambi.

Kutsanula kwa muliri wa chisanu ndi chisanu ndi chimodzi kukubweretsa mphamvu zina ziwiri za chikominisiti pamodzi mu nkhondo ya Armageddoni; koma izi zisanayambe, Mpingo wa Katolika wabwezeretsedwa ku mphamvu monga tinaonetsera kuchaputala cha khumi ndi chitatu. Pamene abwerezetsedwa, nyanga khumi za ku Madzulo kwa Ulaya ndi chikominisiti cha ku Ulaya akudzipereka okha kwa iye ndipo iye akukwera pa chirombo chaku Ulaya, ngakhale kuti nyanga khumi, zidzakhala pa nthawi iyi chikominisiti mu mtima wao. Iwo akudzipereka kwa hule wankulu uyu, chifukwa ali ndi ndalama ndipo akudziwa m'mene angakokere zingwe. Chivumbulutso chaputala 17 chikuonetsera mkazi uyu atakwera pa chirombo ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi, kenako chikuonetsera chirombo chikutembenuka kutsutsana ndi hule wankulu ndi kudana naye ndi kumuotcha ndi moto. Izi ndi kwenikweni kumapeto kwa sabata la 70 la Danieli. Nyanga khumi zomwezo zimene Mpingo wa Katolika ukulamulira zidzamuononga pamene akubwera palimodzi pansi pa komunisti wa ku Ulaya, chikominisiti chao chatsopano, koma Mulungu sadzalora dziko lapansi kuti lilamulidwe ndi mzimu wa chikominisiti uwu. Pakuti ichi chisanachitike, mngelo wachisanu ndi chimodzi akutsanulira muliri wache ndipo ziwanda zimenezo, zimene mpaka pano zakhala zikumvera kachitidwe ka chirombo cha ku Ulaya, tsopano zamasulidwa ndipo zapita Kutali Kum'mawa ndi kulumikizitsa *"mafumu a kum'mawa"* kuchita nkhondo ndi nyanga khumi ndi chikominisiti cha ku Ulaya, ndipo agonjetsedwa ndi nyanga khumi pamene Tsiku la Ambuye likuyamba. **Onetsetsani kuti mukuzigwira izi tsopano: kudutsa mu nthawi yonse ya sabata la 70 la Danieli, mafumu awa a kum'mawa adzakhala akuyang'ana pa kachitidwe ka chirombo. Nyanga khumi za chikominisiti cha Ulaya chikadzangootcha Vatican ndi kuyamba kulamulira,** "mafumu aku M'mawa" iwo adzati, "Ndi nthawi yathu tsopano." **Ndipo iwo adzaika mapulani akugonjetsa dziko lapansi, chifukwa Mulungu waika mafuko a Kutali Kum'mawa uko padera. Pamene Iye adzaitana pa iwo, iwo adzayenda kupita Kum'mawa Chapakati kuchita nkhondo ndi mafumu aku Ulaya awa ndi iwo amene akupanga gawo la kachitidwe ka chirombo, ndipo iwo adzagonjetsedwa mu chidikha cha Megiddo ndi nyanga khumi za ku Ulaya.** Ndiye Khristu ndi Mkwatibwi wake akubwera ku dziko ndi kudzaononga nyanga khumi ndi ankhondo awo. Izi

zikubweretsa chitsiriziro cha chikominisiti kamodzi ndipo nthawi zonse. Chivumbulutso chaputala 19 chikuonetsera m'mene zonse izi zikuchitikira. Ziri momveka uko.

Kodi mukuona lipenga lachisanu ndi chimodzi ndi muliri wa chisanu ndi chimodzi? Lipenga la chisanu ndi chimodzi lidzaomba ndipo lidzaika ankhondo mu chimodzi. Kodi muliri wa chisanu ndi chimodzi udzachita chiyani? Udzamasula kwathunthu ziwanda. Linali dongosolo. Ziwanda zimene zinaikidwa ku malo ena zamasulidwa. Zikupita Kum'mawa Kutali kuchita zozizwa ndi kubweretsa palimodzi mafumu. Ziwanda izi zikuchita zozizwa za ndale ndi kuwabweretsa palimodzi ku nkhondo ya Armageddoni.

Vesi 15: "*Taonani, ndidza ngati mbala. Wodala iye amene adikira, nasunga zobvala zache, kuti angayende wausiwa nangapenye anthu usiwa wache."*

Tithokoze Ambuye chifukwa cha chenjezo limenelo. Ine ndikanafuna kwa Mulungu kuti anthu amvetse chenjezo limenelo. Ine ndikanafuna kwa Mulungu kuti anthu azindikire kuti nthawi iyi yayandikira. Nthawi yayandikira ya zinthu izi. Matchini akhala akugwira ntchito kwa zaka makumi asanu ndi chimodzi apitawa. Ngakhale mbuyo mu Nkhondo Yoyamba ya Dzikolonse ndi Nkhondo Yachiwiri ya Dziko lonse, Mulungu anayamba kuika chithunzi chakumapeto a nthawi. Ngakhale China, mkulu wogona Kum'mawa Kutali, wadzutsidwa ndi kukonzekera nkhondo. Kodi mukuganiza kuti sitiri mu masiku otsiriza? Ndiuzeni m'mene ife tingakhalire ndi m'bado wina; ndiuzeni pamene patsalira nthawi.

Vesi 16: "*Ndipo anawasonkhanitsira ku malo ochedwa m'chihebri Armageddon."*

Ndi nkhondo yaikulu ya Mulungu. Pamene kachitidwe aka sikangathe kugwirana, kenako ziwanda zamasulidwa. **Kachitidwe ka chirombo ku Ulaya kadzagwira mpakana kumapeto kwa sabata la 70 la Danieli. Kutali Kum'mawa kukungokangana wina ndi mzake ndi kungofuna kuyambitsa nkhondo. Lero iwo akuganiza akufuna kuyambitsa nkhondo kumenyana wina ndi mzake, koma sakutero. Iwo akufuna kuyambitsa nkhondo kumenyana ndi nyanga khumi za Kumadzulo kwa Ulaya ndi anzake.**

Padakali muliri umodzi. Pamene muliri uwu utsanulidwa, watsanulidwa mu mulengalenga ndipo mau akuti, "Chachitika"

Vesi 17: "*Ndipo wachisanu ndi chiwiri anatsanulira mbale yake mumlengalenga; ndipo m'Kachisi mudatuluka mau akuru, ochokera ku mpando wachifumu ndi kunena, chachitika."*

Vesi 18: "*Ndipo panakhala mphezi, ndi mau, ndi mabingu; ndipo panali chivomerezi chachikuru chotero sichinaoneke chiyambire anthu padziko, chibvomerezi cholimba chotero, chachikuru chotero."*

Ichi ndi chivomerezi chomwecho chimene chikulankhulidwa pansi pa chisindikizo chachisanu ndi chimodzi ndi pakuomba pa lipenga lachisanu ndi chiwiri; ichi ndi kukwaniritsidwa kwenikweni kwa icho monga alembera apa.

Vesi 19: "*Ndipo chimudzi chachikurucho chidagawika patatu, ndi midzi ya amitundu inagwa; ndipo Babulo waukuru unakumbukika pamaso pa Mulungu, kuti aupatse chikho cha vinyo wamkali wa mkwiyo wake."*

Taonani chiweruzo cha Mulungu chikuchitika. Ndikungopitiriza kwa chiweruzo cha Mulungu Wamphamvuzonse. Chiweruzo chimene chayamba kale pa Katolika ndi Chiprotestant chafika kumapeto apa. Miriri iyi ikuchitika pafupipafupi. Ziri ngati kukhala ndi chimulu ndikukhuthulira pa gasoline ndi kuchiyatsa, ndipo moto usanazime ndikutsanuliranso wina ndi choncho; mpakana mbale zisanu ndi ziwiri zodzala ndi mkwiyo wa Mulungu zatsanulidwa pa dziko kutsiriza mkwiyo wa Mulungu. Dziko likufika ku maonekedwe oti izi zichitike tsopano. Muliri uwu wa chisanu ndi chiwiri ukufotokoza za Babulo kubwera ku chikumbutso pa maso pa Mulungu kumupatsa iye chikho cha vinyo wa kuopsa kwa mkwiyo wa Mulungu. Chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chiwiri ndi chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chitatu chikutiuza m'mene Mulungu akuweruzira Babulo. Komanso, mizinda ya mafuko inagwa pa nthawi iyi. Kuonetsera muliri uwu ndi chiweruzo cha dziko lonse cha Mulungu.

Vesi 20: "*Ndipo zisumbu zonse zidathawa, ndi mapiri sanapezeka."*

Pamene chivomorezi chikuchitika, padzakhala kwenikweni nzere wa mapiri umene sudzaoneka. Padzakhala zisumbu zimene zidzasowa. Kodi ndi chiyani? Ndi Mulungu kukonzanso pamwamba pa dziko kukonzekera mileniamu, monga m'mene anachitira mu masiku a Nowa pamene Iye anatumiza chiweruzo pa dziko lapansi.

Vesi 21: *"Ndipo anatsika kumwamba matalala akuru, lonse lolemera ngati talenti, nagwa pa anthu; ndipo anthu anchitira Mulungu mwano chifukwa cha muliri wa matalala, pakuti muliri wake ndi waukuru ndithu."*

Sikunali chivomerezi chachikulu chokha, sikungoti dzuwa linada kokha, osati zochitika izi zokha, koma miyala ya matalala inayamba kugwa kuchokera kumwamba. Muliri unatsanulidwa mulengalenga ndipo mau anati, "chachitika." Taonani chimene chinachitika. Chilengedwe chonse chinagwedezeka, dziko linayamba kuchita phokoso, mapiri akugwa, ndi zisumbu kusowa. Osati zokhazo; komanso gawo la mwamba lidakhudzidwa chifukwa kumeneko ndi kumene muliri unatsanuridwa. Matalala anayamba kugwa pa dziko, matalala amene anthu sanawaonepo chiyambire. Kodi mukutha kuona Mulungu akutsiriza m'bado uno ndi kuweruza dziko lapansiri, ndi kuweruza m'bado uno umene wamukana Iye?

Tsopano tiyeni tifananitse lipenga lachisanu ndi chiwiri. Chivumbulutso 11:15-*"Ndipo mngelo wachisanu ndi chiwiri anaomba, ndipo panakhala mau akulu m'mwamba, ndi kunena, Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Khristu wache: ndipo adzachita ufumu kufikira nthawi za nthawi."*

Lipenga lachisanu ndi chiwiri iri likutsegula nyengo ya nthawi, ndipo likupereka ngakhale momveka kumene Mulungu adzatengere ichi pamene chiyamba. Chimene ichi chikuonetsera ndi chakuti pamene chiyamba sichidzaima mpakana Mulungu atayeretsa dziko lapansi, kuweruza ilo, ndi kudzutsa akufa amene anaphedwa mu nyengo ya chisautso. Izi zikuchitika pamene Khristu akubwera kudzalamulira mu Mileniamu.

Chivumbulutso 11:18- *"Ndipo amitundu anakwiya, ndipo unadza mkwiyo wanu, ndi nthawi ya akufa kuti aweruzidwe, ya kupereka mphotho akapolo anu aneneriwo, ndi oyeramtima, ndi iwo akuopa dzina lanu, ang'ono ndi akulu; ndi kuononga iwo akuononga dziko."*

Tsopano, pamene tikufananitsa lipenga lachisanu ndi chiwiri ndi muliri wa chisanu ndi chiwiri, taonani kufanana. Chivumbulutso 11:19- *"Ndipo anatsegulidwa kachisi wa Mulungu amene ali m'mwamba; ndipo linaoneka likasa la chipangano chache, m'kachisi mwache, ndipo panali mphenzi, ndi mau, ndi mabingu, ndi chibvomerezi, ndi matalala akulu."* Kodi chinachitika ndi chiyani pansi pa muliri wachisanu ndi chiwiri? Chivomerezi, matalala akulu, mphenzi, ndi zina zotero. Pansi pa lipenga lachisanu ndi chiwiri ndi pansi pa muliri wa chisanu ndi chiwiri zikudutsa mu chinthu chomwecho zinadutsamo mu pansi pa lipenga la chisanu ndi chimodzi chifukwa zonse zinachitika mu nyengo yomweyo ya nthawi imene kuomba kwa lipenga lachisanu ndi chiwiri linatsegula. Zikuonetsera zonse zikutha sabata la 70 la Danieli litatha.

Muliri woyamba unatsanulidwa pa anthu ndipo unayambitsa zironda zikuluzikulu. Muliri wachiwiri unasandutsa nyanja mwazi. Muliri wachitatu unasandutsa mtsinje kukhala mwazi. Pansi pa muliri wa chinai, dzuwa linadetsa anthu. Pansi pa muliri wa chisanu, m'dima ndi chisokonezo zinatsanulidwa pa mpando wa chirombo. Pansi pa muliri wa chisanu ndi chimodzi, mtsinje wa Firate moyimirira unauma; ndipo mafuko amene lipenga lachisanu ndi chimodzi linabweretsa pamodzi anayenda mu chigwa cha Megiddo kuchita nkhondo ya Armageddoni. Muliri wa chisanu ndi chiwiri unatsanulidwa ndipo mau anati, "Chachitika. Uwu ndiwo mkwiyo onse wa Mulungu. Palibenso wina wotsala."

Tsopano, tisanatseke chaputala ichi, ine ndikufuna ndikhutire kuti mumvetsa pamene muliri wachisanu ndi chiwiri uwu utsanulidwa, ndi *kumapeto* kwa kutha kwa sabata la 70 la Danieli. Miriri isanu ndi umodzi yachitika sabata la 70 la Danieli *lisanathe*. Kenako Tsiku la Ambuye likuyamba muliri wachisanu ndi chiwiri ukangotha kutsanulidwa kutsiriza mkwiyo wa Mulungu. Ndi chisindikizo chachisanu ndi chiwiri kukwaniritsidwa. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHISANU NDI CHIWIRI

Vesi 1: *"Ndipo anadza m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri, nalankhula ndi ine, nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsa chiweruzo cha mkazi wa chigololo wamkulu, wakukhala pa madzi ambiri."*

Taonani: *"m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri."* Muli vumbulutso mu zimenezo. Angelo asanu ndi awiri amenewo ali ndi gawo lofunika kwambiri. Uyu ndi m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri auzimu kumuonetsera Yohane chiweruzo cha hule wankulu amene akhala pa madzi ambiri. Hule wamkuluyu ndi Mpingo wa Katolika wa Chiroma. **Hule wankulu m'modzi,** monga tidzawerenga patsogolo mu chaputala ichi, iye ali ndi ana akazi. Ana akazi awa ndi mahule ndipo alipo ambiri aiwo. Iwo akupanga fano la chirombo, ndipo ali mipingo ya Chiprotestanti. Monga Yohane ali mu masomphenya ake, mngelo akuyamba kumuuza iye, "Idza kuno, ine ndikufuna ndidzakuonetse chiweruzo cha hule wankulu uyu."

Vesi 2: *"Amene mafumu a dziko anachita chigololo naye, ndipo iwo akukhala pa dziko analedzera ndi vinyo wa chigololo chache."*

Izi zikukamba za chigololo cha uzimu. Taonani kuti mafumu a dziko lapansi achita chigololo. **Paliponse pamene Mpingo wa Katolika wa Chiroma ukupita, umagona ndi mafumu a dziko lapansi. Iye amamanga ma sukulu, zipatala, ndi zina zotero, ngati njira yolowera mu boma,** ndipo akuti anthu okhala pa dziko aledzera ndi vinyo wa chigololo chake. Kodi vinyo wa chigololo chake ndi chiyani? Ndi chiphunzitso chake. Iwo aledzera, pali ambiri lero amene adzakuphani chifukwa cha chiphunzitso chawo. Iwo achita chigololo cha uzimu ndi iye, ndiye mu uhule wake ali nawo ana akazi.

Vesi loyamba likuti, *"Ndidzakuonetsa chiweruzo cha hule wankulu."* Sikungoti akuonetsera chiweruzo cha hule wankulu, komanso akulankhula chinachake chokhudza hule wankulu iye asanayambe kuuza Yohane chimene chiweruzo chake chidzakhale. Ife tikudziwa m'mene chiweruzo chake chidzakhalire pamene Mau akufotokoza mochuluka mu chaputala ichi.

Vesi 3: *"Ndipo ananditenga kupita nane ku chipululu, mu Mzimu; ndipo ndinaona mkazi alikukhala pa chirombo chofiiritsa, chodzala ndi maina amwano, chakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi."*

Apa pali mkazi wokhala pa chirombo chofiira. **Ine ndikufuna ndisiyanitse, makamaka, mkazi ndi chirombo.** Ife tikuyenera kuchita zimenezo kuti inu muone chithunzithunzi cha kumapeto ndi chimene chiti chichitike, ngakhale mu m'bado wathu omwe uno.

Hule wankulu *akukwera* pa chirombo. Chirombo ichi chiri chodzala ndi maina a mwano, kuchitira mwano Mulungu wa kumwamba pokhala ndi udindo umene ndi wa Mulungu yekha. Pamene mafumu awa analowa mu mzinda wa Roma, kapena kulikonse anapita, adani awo ameyenera kuwalambira iwo, ndi iwo amene akanatha, mpakana kupsopsona mapazi a mafumu. Zimenezo zimachitika mu Ufumu wa Chiroma monga zinayambira kale mu nthawi ya ma B.C.

Apa, mkazi wakhala pa chirombo kuchiyendetsa icho. Mkazi ali ndi ulamuliro pa chirombo ichi. **Pamene aliyense akuyendetsa chirombo, ndiye akuchilamulira chirombocho.** Kotero mkazi uyu ali ndi ulamuliro pa chirombo chimene mngelo akumuonetsera Yohane. Chirombo chimene mkazi uyu akuchiyendetsa chiri chodzala ndi maina amwano. Kodi maina a mwano amenewa ndi chiyani?

A Kaesara akale amadzitcha okha "Wolamulira." Wolamulira ali ndi tanthauzo ngati, "*Woimapayekha, wolamulira paliponse."* Inu mukhoza kungoika udindo umenewo pa m'modzi, ndipo ndi Mulungu yekha. Ma Kaesara awa amene analamulira mu masiku oyambirira anadzitchula okha "Wolamulira." Palibe munthu amene ndi olamulira paliponse. Palibe munthu amene ndi woima payekha pa dziko lapansi. Kotero, olamulira awa a ku Roma anadzitchula okha olamulira a dziko lapansi.

"Kuimapawekha" zikutanthauza kuti uli ndi chinachake. Ndi chifukwa chake Mulungu ndi woima payekha. Ndi pa Mulungu yekha pamene inu mungagwiritse ntchito mau oti "Woimapayekha" chifukwa ndi Mulungu yekha amene ndi woima payekha pa dziko, kapena pa dziko lonse. Pali chirombo apa chodzala ndi maina a mwano; ndi maudindo amene wolamulira a ku Roma amagwiritsa ntchito. Tsopano ndi papa amene amagwiritsa ntchito maudindo a mwano.

Ine ndawerenga kwambiri za mbiri ya Ulamuliro wa Chiroma, koma sikuti ndikupatsani phunziro la Roma. Pali zambiri zolembedwa za izo, koma ine ndikufuna ndikuonetsereni chinachake chokhudza mzinda wa Roma chifukwa ndi mpando wa chirombo.

Mzinda wa Roma unapezedwa ndi amuna achichepere awiri wotchedwa Romelus ndi Remus cha mu pafupifupi 800 B.C. Roma amangoyamba kumene pamene Babulo anali alipo. Roma amakhala pakati pa mapiri asanu ndi awiri. Lirilonse la phiri liri ndi dzina lache. Ngakhale kuti mzinda wa Roma unayamba cha m'ma 800 B.C., Ukaesara wa Roma sunayambe mpakana m'ma 180 B.C. Ena mwa a Kaesara anali

Julias, Augustus, Clandia, Cicero, ndi Nero, amene anali wotsiriza mu mzere umenewo wa ma Kaesara. Ichi chinapanga mutu umodzi waukulu pa chirombo umene Daniel anauona. Izi zikutanthauza kuti ngakhale kuti Yohane anaona chirombo chomwechi chokhala ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi, idzakhala dera lomwelo; chifukwa Danieli adaona nyanga khumi pa mutu waukulu. Kuchokera mwa mutu umodzi uwu waukulu mukuchokera mitu iyo imene Yohane anaiwona. Zimene zaonetseredwa ndi vesi la khumi.

Roma anali kale mphamvu ya dziko pa nthawi imene Khristu anabwera ku dziko. Chaputala ichi cha khumi ndi chisanu ndi chiwiri cha Chivumbulutso chikutipatsa ife kuonanso za Ulamuliro wa Roma.

Cholinga chimene ine ndikufuna kuti muone mzinda wa Roma ndi dera la ulamuliro wa Roma ndi chifukwa chakuti mkazi akukwera pa chirombo. Kenako chirombo chikumuononga mkazi. Ine ndikufuna ndisiyanitse ichi, chifukwa pamene anthu alankhula za Mpingo wa Katolika wa Chiroma, iwo amangoti Roma kapena chirombo, ndipo amasiya mafunso osayankhidwa ambiri.

Inde, apa ndi pamene anthu amasokoneza. Inu mwazimva zikulalikidwa nthawi zambiri kuti mpingo wa Katolika ndi chirombo, ndi zina zotero, koma kachitidwe aka ka chirombo kanayambika mu 800 B.C. Chirombo chachinai, mzinda wa Roma, unayamba kumamangidwa kenako. **Mpingo wa Katolika wa Chiroma sunayambe mpakana zaka 1100 patsogolo pake. Tsono, Mpingo wa Katolika wa Chiroma ungakhale bwanji chirombo?** Mkazi, Mpingo wa Katolika , ukukwera pa chirombo. Ine ndikufuna kupanga kusiyana uku chifukwa inu muona chirombo, nyanga khumi, zikuononga mkazi, hule. Nyanga khumi sizingaziononge zokha, zingatero? Mkazi uyu anazikometsera ndi golidi, ndi miyala ya mtengo wache ndi ngale. Iye anadzikometsera ndithu. Iye akukhala wapamwamba. Awa anali masomphenya amene Yohane adawaona ndipo anamutcha iye hule wankulu.

Vesi 4: *"Ndipo mkazi anavala chibakuwa, ndi mlangali, nakometsedwa ndi golidi, ndi miyala ya mtengo wache, ndi ngale; nakhala nacho m'dzanja lache chikho chagolidi chodzala ndi zonyansitsa, ndi zodetsa za chigololo chache."*

Mtundu wofiira ndi mtundu wa chifumu wakale wa Kaesara. Taonani kuti mkazi wavala chofiira ndi mlangali,kuonetsera kulumikizana kwa mphamvu ziwirizi. Ndani anazirumikizitsa? Konsitantine analumikizitsa mpingo ndi boma palimodzi mu 325 A.D. Mkazi si chirombo; mkazi akukwera chirombo. Panali chirombo zaka mazana mazana Mpingo wa Katolika wa Chiroma usanakhale.

Vesi 5: "*Ndipo pamphumi pache padalembedwa dzina*, CHINSINSI, BABULO WANKULU, AMAI WA ACHIGOLOLO NDI ZONYANSITSA ZA DZIKO."

Iye anali hule mwiniyekha ndipo anali mai wa mahule. Ine ndikufuna ndinenenso, ichi si chirombo. Ayi, iye *akukwera* chirombo chachinai cha pa Danieli chaputala chachisanu ndi chiwiri. Danieli anachiona icho makamaka pamene chinadzuka ndi mutu umodzi waukulu ndipo anali a Kaesara akulu mu nyengo ya ma B.C. Kodi chirombo chikanatha bwanji kukhala Mpingo wa Katolika wa Chiroma, ngati chirombo chinalipo zaka mazana mazana mbuyomo mpingo wa Katolika usanayambe? Chirombo chachinai chikuononga Mpingo wa Katolika. Mpingo wa Katolika unatenga ulamuliro mu Nthawi ya M'dima ndi kutsitsa atatu mwa mafumu ndi kukwapula Ulaya. Mafumu amayenera kumuopa iye, koma nthawi zambiri samafuna kutero. Ambiri anayesera kumuukira, ndipo iye amamasula adani ake a mfumu imeneyo. Ndipo anthu amangopita ndi kusankha mfumu ina. Mwa kulankhula kwina, mkazi amene amakhala pa chirombo anali ndi ulamuliro wonse, kapena kuti "cholumira pakamwa" mukhoza kunena. Iye amalamulira chirombo.

Taonani vesi lachisanu likuti, pamphumi pache panali dzina lolembedwa, "CHINSINSI, BABULO WANKULU, AMAI WA ACHIGOLOLO NDI ZONYANSITSA ZA DZIKO." Iye anali hule wankulu, ndipo anali ndi ana akazi.

Hule akukwera chirombo. Taonani izi, palibe m'modzi mwa ana akazi akukwera chirombo. Mai akukwera chirombo ndipo ali ndi dzina, "CHINSINSI BABULO." Zalengezedwa kwa Yohane, "Iye ndi mai wa mahule."

Taonani, **palibe m'modzi mwa ana akazi akukwera chirombo,** koma mai wa mahule yekha. Kodi mwachigwira chimenecho? Chifukwa chiyani? **Ana akazi amalamulira kuno ku United States ngati "fano la chirombo."** Onse timahule tating'ono timakhala pamodzi, ndipo chirombo chamwanawankhosa cha pa Chivumbulutso chaputala 13 chimawapatsa mphamvu kulankhula zimene ziri zolondora kapana

zosalondolora mu gawo la uzimu. Iwo akulamulira kuno ku United States pamene "Mai" akulamulira Kumadzulo kwa Ulaya ndi dziko la uneneri. Ndi chifukwa chake Baibulo likuti osati kulambira **chirombo kapena fano lache.** Akusiyanitsa pakati pa mai ndi ana ake.

Vesi 6: *"Ndipo ndinaona mkazi woledzera ndi mwazi wa oyeramtima, ndi mwazi wa mboni za Yesu; ndipo ndinazizwa pakumuona iye ndi kuzizwa kwakukulu."*

Vesi 7: *"Ndipo mngelo anati kwa ine, Uzizwa chifukwa ninji? Ine ndidzakuuza iwe chinsinsi cha mkazi, ndi cha chirombo cha kumubereka iye, chokhala nayo mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi."*

Mukugwira kusiyana kwa zinthu ziwiri izi: Mkazi, ndi chirombo chimene chinamutenga iye. Chirombo chimene chinamutenga mkazi chiri ndi mitu isanu ndi iwiri komanso nyanga khumi. Ichi ndi chirombo chomwecho Danieli anachiona; Koma Danieli sanaone mkazi akukwera pa chirombo. Iye anangoona kanyanga kena kakang'ono kakutuluka. Mkazi uyu waledzera ndi mwazi wa oyeramtima. Iye ndi wakupha ndipo sadzalapa. **Mkazi uyu ndi Mpingo wa Katolika wa Chiroma. Mafuko khumi aku Ulaya ndi iwo amene akukhudzidwa ndi chirombo chimene mkazi uyu akukwerapo.**

Vesi 8: *"Chirombocho unachiona chinaliko, koma kulibe, ndipo chidzatuluka mphompho, ndi kunka ku chitaiko. Ndipo adzazizwa iwo akukhala pa dziko amene dzina lawo sirinalembedwa m'bukhu la moyo chiyambire makhazikidwe a dziko lapansi, pakuona chirombo, kuti chinaliko, ndipo kulibe, ndipo chidzakhalako."*

Taonani, pali chirombo chimene chikutuluka kuchokera ku phompho. Tiyeni tione zimenezo kanthawi pang'ono. Kodi ndi chiyani chikutuluka ku phompho? Ndi mzimu wa mdierekezi mu kachitidwe ka mpingo. Palibe chirichonse chogwirika chikutuluka mu phompho. Awa ndi masomphenya Yohane adawaona; Mulungu akufuna ife tikhale ndi kumasulira kwa izo.

Mulungu amalora mdierekezi kulowa mu kachitidwe. Aka ndi kachitidwe kakakulu kamene dziko lonse lapansi likhoza kuona. Iwo sangaone mzimuwo pamene ukumasuludwa ndi kuloredwa kubwera pa dziko.

Kodi chirombo ichi ndi chiti chimene chinaliko, ndipo kulibe, ndipo chiripo? Kodi mukudziwa chimene chimayankha funso limenelo? Chivumbulutso 13 chikutiuza ife. Ufumu wa Chiroma unali wosefukira tisanafike m'ma 1500 A.D., ndipo papa amalamulira Kumadzulo kwa Ulaya; ndi pamene chirombo *"chinali."* Chirombo chimenecho chimalamurira Ulaya mu M'bado wa M'dima, koma nthawi inafika kuti Mulungu abwezeretse chidziwitso cha Mulungu ku Mpingo. Martin Lutera anatuluka ndi lupanga lalikulu ndi kukhapa mutu uwu wa chisanu ndi chiwiri wa chirombo chimenecho mpakana chinali pafupifupi kufa. Chirombo *"chinaliko"* nthawi iyi isanafike, ndipo pamene Martin Lutera anachikhapa, chirombo *"kunalibe."*

Napoleon anatumiza mkulu wa nkhondo wache ndi kumuchotsa pa mpando papa; ndipo kunali kulankhula ku Ulaya kuti "Upapa wafa ndipo palibe amene adzatukula chala kuthandizira izo." Zimenezo zinali mu 1798 pamene Napoleon natumiza nkulu wankhondo wache ndi kuchotsa pa mpando papa.

Chirombo *"kunalibe"* chatha, komabe mzinu wa chinthuchi unali ulipobe mu njira yonse. Chirombo *chinaliko,* ndipo *kulibe,* ndipo *chiriko,* chidzatuluka kuphompho kachiwirinso mu masiku otsiriza ndi kudzakhala mpaka chitapita ku chionongeko. Ndi kubwezeretsedwa kwa Ulamuliro wa Chiroma oyang'aniridwa ndi papa monga zinaliri mu nthawi ya kukonzanso, pamene Mulungu akulora Mpingo wa Katolika wa Chiroma kubwezeretsedwa mu mphamvu yake yonse. Mafuko khumi amenewa adzadzipereka kwa papa pamene Mulungu akumulora papa pa mpando wachifumu amene amadziwa kukoka zingwe, ndipo adzapanga pangano ndi mafuko ambiri zimene zidzakhala zaka zisanu ndi ziwiri, koma pakati pa sabata, iye adzaphwanya pangano ndipo zimenezo zikubweretsa nyengo ya chisautso ku gawo lachiwiri la sabata la 70 la Danieli. Chirombo chimenecho chidzalamuliranso Ulaya ndi dziko lapansi. Mtundu wa anthu udzati kuti ndi chinthu chachikulu chimene sichinakhalepo; kupatula iwo amene maina awo analembedwa mu bukhu la Mwanawankhosa wa moyo dziko lapansi lisanalengedwe. **Apo pali chirombo chimene chinali, ndipo kulibe, ndipo chiripo, chimene chidzatuluka ku phompho, ndi kupita ku chionongeko, ndipo dziko lapansi lidzadabwa nacho.**

Vesi 9: *"Pano pali mtima wakukhala nayo nzeru. Mitu isanu ndi iwiri ndiyo mapiri asanu ndi awiri amene mkazi akhalapo."*

Mzinda wa Roma uli pakati pa mapiri asanu ndi awiri monga tonse tikudziwira, ndipo ndi pamene Vatican, likulu la Mpingo wa Katolika wa Chiroma liri.

Vesi 10: *"Ndipo ali mafumu asanu ndi awiri, asanu adagwa, imodzi iriko, yinayo siinadze; ndipo pamene ifika iyenera iyo kukhala kanthawi."*

Mafumu asanu ndi awiri akuimirira mitundu yosiyana isanu ndi iwiri ya boma la Chiroma, zimene muli zolembedwa zambiri za zimenezo ndipo sitingathe kuziika mu bukhu iri, koma ine ndikufuna ndikuonetsereni inu kuti izi ndi nyengo ya ma Kaesara itatha imene Nero anali wotsiriza. Pamene iye anafa mu 68A.D. mutu umodzi mu maonekedwe amenewo unafika kumapeto. Pakati pa nthawi iyi ya mutu waukulu pa chirombo monga Danieli anachionera icho ndi mitu isanu ndi iwiri imene Yohane anaona, pali chimene chikutchulidwa mu mbiri kuti Akaesara achi Flavian. Chifukwa Nero atamwalira, panalibe m'modzi mwa abale ake otenga mpando wa chifumu. Kotero nyumba ya malamulo ya Chiroma inatumiza Flavius Vesasianus, nkulu wa gulu la nkhondo amene anali ku Yerusalemu, kumupanga iye wolamulira wa Ufumu. Vesasianus kenako anapanga Tito kukhala nkulu wa gulu la nkhondo ku Yerusalemu amene anaononga mzinda wa Yerusalemu mu 70A.D. Kenako Venasianus atafa, Tito anatenga mpando wa chifumu, ndipo Tito atafa, Domitian, m'modzi mwa ana a Vesasianus , anatenga mpando wa chifumu, ndipo ulamuliro wache ukutitengera ku nthawi imene Yohane anali ndi masomphenya amene tikuwaphunzira mu vesi la khumi la chaputala ichi.

Mu 96 A.D. Yohane anaona chirombo chomwechi chimene Danieli adaona, koma pamene Yohane adachiona chinali ndi mitu isanu ndi iwiri. Kotero, muzobisika, apa pali chimene chinachitika. Kuchokera pafupifupi 96A.D. mpakana 180 A.D. panali olamulira asanu, osati a Kaesara, amene akudziwika mu mbiri ngati "Olamulira asanu agolidi." Taonani kuti iwo adzabwezeretsanso udindo womwewo wa mwano pomatchulidwanso olamulira. Mbiri imapereka maina awo, woyamba anali Nerva, wachiwiri anali Trajan, wachitatu Hadrian, wachinai Antonius Pius, ndipo wachisanu anali Marcus Aerelius. Izi zikutibweretsa ife ku cha m'ma 180 A.D.; ndipo ndi tanthauzo la *"asanu agwa"* mu vesi la khumi. Izi zachuluka, koma ine ndikuyenera kuzichita njira imeneyi; sindikulemba bukhu la mbiri. [Tadziwani: zikuchokera ku zolemba za Raymond Jackson]

Kuchokera 180 A.D. mpakana 300 A.D. kunali nthawi yosautsa, ndipo olamulira ambiri anaphedwa mu nthawi iyi. Kenako inabwera nthawi ya Konsitantini. Iye anapambana pa kubweretsa malamulo ku Ulamuliro wa Chiroma polumikizitsa mpingo palimodzi ndi boma. Inu mukhoza kuzikumbukira izi powerenga za mpingo wa m'bado wa Pergamo. Iyi ndi nthawi yoyamba imene boma linakhalapo losakanikirana ndi Chikhristu ndi boma la anthu. Iyi ndi mfumu ya chisanu ndi chimodzi kapena mtundu wa boma la Chiroma lachisanu ndi chimodzi Yohane analiona boma la mutu waukulu limodzi mu masomphenya a Daniel litatha. Iri ndi tanthauzo la *"m'modzi alipo"* mu vesi la khumi, ndipo zikuika poyambira pa mitu isanu ndi iwiri kapena ufumu umene unayamba mu 600 A.D. ndipo unali mu dongosolo iri. Pamene mpingo ndi boma zinayamba kugwira ntchito palimodzi ndipo mtundu wa Chikhristu umenewo unafalikira mu Ulamuliro wa Chiroma onse, udindo wa upapa unaikidwa mu nthawi iyi, ndipo panayamba kukhala funso la amene anali ndi mphamvu, olamulira kapena papa. Panthawi iyi madera ena mu Ufumu wa Roma anayamba kuchoka, mpakana unaphwanyika kukhala nyanga khumi zimene tikuziphunzira mu bukhu iri. Izi zinapanga mfumu ya chisanu ndi chiwiri kapena mutu mu kachitidwe ka chirombo pamene papa anatenga ulamuliro pa olamulira. M'modzi mwa ma papa anatulutsa zitatu mwa nyanga pansi pa kachitidwe kameneka ka boma la Chiroma. Iye anachotsa pampando atatu mwa mafumu ndi kumasula adani ake, koma atatha kulapa ndi kudzipereka okha kwa papa, iye anawabwezeretsa ngati mafumu mu madera awo. Umenewo ndi mutu wa chisanu ndi chiwiri umene Yohane adauona ndipo ndi umene unalandira bala lakuimfa ndipo unakhala ndi moyo. Ndi amene *"akupitiriza mu kanthawi pang'ono"* mu vesi la khumi.

Vesi 11: *"Ndipo chirombo chinalicho, ndi kulibe, icho chomwe ndicho chachisanu ndi chitatu, nichimuka kuchitayiko."*

Monga mkazi wakwera pa mafuko a ku Ulaya, mutu wa chisanu ndi chitatu [mzimu] ukutuluka kuchokera kuphompho. Palibe m'modzi mwa mafumu amene akutuluka ku phompho. Palibe m'modzi mwa mapapa amene akutuluka mu phompho. Koma ndani akutero? Satana mwiniwake, mzimu wa chirombo wa chinthu ichi, ukutuluka kuchokera ku phompho. Iye ndi wachisanu ndi chitatu, koma pa asanu ndi awiri. Mtundu wachisanu ndi chiwiri wa boma la Chiroma linali mafuko khumi ndi awiri aku Ulaya **ndi papa ngati wowalamulira.** Ndi iye amene anapitiriza kanyengo pang'ono ndiye kenako

analandira bala la kuimfa. **Umodzi wa mitu yake inavulazidwa ku imfa, koma bala la ku imfa linachiritsidwa, kutanthauza kuti mtundu wa chisanu ndi chiwiri wa boma la Chiroma udzabwezeretsedwa pamene mafuko khumi awa akumvera papa.** Osati mafuko khumi okha, koma zidzakokeramo maufumu ena a zirombo zina. Yohane anaona chirombo ku Chivumbulutso 13 ngati nyalugwe, kambuku, ndi mkango.

Vesi 12: *"Ndipo nyanga khumi udaziona ndiwo mafumu khumi, amene sanalandire ufumu; koma alandira ulamuliro ngati mafumu, ora limodzi, pamodzi ndi chirombo."*

Nyanga khumi ndi mafuko khumi a ku Ulaya amene ali ndi ulamuliro pa nthawi ino pansi pa papa, koma monga Chivumbulutso chaputala 16 chationetsera ife, ku mapeto akumuononga hule. Kodi chirombo chinachokera kuti? Icho chinachokera ku phompho. Nyanga khumi zikulandira mphamvu kuchokera ku chirombo chimene mkazi anakwera.

Vesi 13: *"Iwo ali nao mtima umodzi, ndipo apereka mphamvu ndi ulamuliro kwa chirombo."*

Nyanga khumi sizikugwirizana ndi kukondana, koma sizingaimitse mau a Mulungu. Ine ndikukuwerengerani mbiri imene siinakwaniritsidwe. Limodzi mwa masiku amenewa mafuko khumi aku Ulaya amenewo aku Madzulo kwa Ulaya adzagwirizana kwathunthu pa choti achite. Kodi mukudziwa kuti kugwirizana kwathunthu kumeneko kudzakhala chiyani? Iwo adzati, "Tiyeni timvere papa; tiyeni timvere Mpingo wa Aroma." Iwo adzadzipereka kwa hule ndipo hule adzakwera pa iwo. Iwo adzakhala ndi lingaliro limodzi. Iye adzakokera ulamuliro kumanzere ndipo onse adzapita kumanzere. Iye adzakokera ulamuliro kumanja ndipo onse adzapita kumanja. Iwo adzakhala ndi lingaliro limodzi, chifukwa ndi Mau a Mulungu. Ndi mutu wachisanu ndi chitatu wa uzimu wa mu vesi 11 kukwera mtundu wa chisanu ndi chiwiri wa boma la Chiroma. Ndi satana, mdierekezi, mneneri wonama, kupyolera mwa kachitidwe ka chirombo ka Roma, kupyolera mwa ulamuliro wa Chiroma. Nyanga khumi zimenezi zidzakhalanso ndi lingaliro limodzi pa zokhudza chiononge ko cha hule wankulu ndi chipembedzo chonse. Kenako, pamene Yesu abwera ku dziko ndi Mkwatibwi wake, iwo akuyesera kuchita nkhondo ndi Iye ndi Mkwatibwi Wake.

Vesi 14: *"Iwo adzachita nkhondo pa Mwanawankhosa, ndipo Mwanawankhosa adzawalaka, chifukwa ali Mbuye wa ambuye, ndi Mfumu ya mafumu; ndipo adzawalakanso iwo akukhala naye, oitanidwa, ndi osankhika ndi okhulupirika."*

Taonani, *"Iwo adzachita nkhondo pa Mwanawankhosa."* Kodi iwo adzachita liti izo? **Osati pamene hule akukwera pa iwo, koma atatha kupha hule. Kenako iwo adzachita nkhondo ndi Mwanawankhosa; ndi Chivumbulutso 19.**

Mu vesi loyamba, mngelo anamuuza Yohane kuti akanadzamuonetsa iye chiweruzo cha hule; koma taonani zimene iye anadutsamamo asanamuonetse Yohane chiweruzo cha hule wankulu. Iye anaonetsa mogwirika Ufumu wonse wa Aroma kwa Yohane.

Vesi 15: *"Ndipo anena ndi ine, Madziwo udawaona uko akhalako mkazi wa chigololoyo ndiwo anthu, ndi makamu, ndi mitundu, ndi manenedwe."* [Mpingo Aroma udzalamulira dziko lonse la UNENERI.]

Vesi 16: *"Ndipo nyanga khumi udaziona, ndi chirombo, izi zidzadana ndi mkazi wa chigololoyo, nizidzankhalitsa wabwinja wausiwa, nizidzadya nyama yache, nizidzampsereza ndi moto."*

Tsopano, ine ndikufuna ndikuonetsereni chiweruzo cha hule wankulu. Nyanga khumi izi zidzadana ndi hule. Mtundu wa chisanu ndi chiwiri uwu wa boma la Chiroma umene Mpingo wa Katolika wa Chiroma ukulamulira pakadali pano ndi wa Chikoministi mu mzimu wao, mu mitima yawo. Chikominisiti chalowerera mu maboma a ku Ulaya. Inu mukudziwa zimenezo chifukwa inu mumazimva zimenezo mu nkhani ndi kumawerenga mu ma pepala, koma iwo adzadzipereka okha kwa hule. Iwo adzadzipereka ndi kugona ndi hule.

Chinthu chimodzi cha izo, mafumu atatha kukhala ndi hule kwa nthawi, iwo anatopa naye ndi kufuna kuthana naye. Palibe aliyense amene angafune kukhala ndi hule, alipo otero? Kotero pakapita ka nthawi, iwo adzadana ndi hule. Pamene iwo aona kuti ndi mtundu wanji wa hule iye ali, adzatopa naye. Iwo akudana naye hule, kumupanga iye kukhala wa maliseche, ndi kumuotcha iye pa moto.

Mafuko khumi aku Ulaya amenewo ndi Chikominisiti cha ku Ulaya zidzaononga Mpingo wa Katolika wa Chiroma; iwo adzaononga chipembedzo monganso dziko lapansi. Kodi Mpingo wa Katolika wa

Chiroma udzaonongedwa? Inde. Ine ndikukuwerengerani inu mbiri imene siinakwaniritsidwe, koma idzakwaniritsidwa. Chifukwa chiyani adzachita zimenezo? Vesi 17 likutiuza chifukwa chake.

Vesi 17: *"Pakuti Mulungu anapatsa kumtima kwao kuchita za kumtima mwache, ndi kuchita cha mtima umodzi ndi kupatsa ufumu wao kwa chirombo, kufikira akwaniritsidwa mau a Mulungu."*

Mulungu akuika mwa mafumu awa mitima yopereka mphamvu zawo kwa chirombo, kuti Mau Ake akwaniritsidwe. Hule ameneyi adzaonongedwa ndi Chikominisiti cha ku Ulaya.

Lingaliro ku utumiki wa mu nthawi yotsiriza: Ngati Mulungu angathe kutenga mafuko khumi amenewa amene ndi achikoministi ndipo sadziwa Mulungu, ndipo akhoza kuwapanga iwo kuchita chimene Iye akufuna iwo achite, kukwaniritsa Mau Ake, ndiye, angatipange bwanji ife amene tiri ndi Mzimu Woyera, amene tiri ndi lingaliro la Yesu, amene tikuvutikira kuchita chifuniro Chake, ndi kutibweretsa ku umodzi wathunthu ndi kutipanga ife tonse kukhulupirira chinthu chimodzi. Ngati Mulungu angathe kutenga dziko la chikominisiti iri, kuikapo dzanja lake, ndikuwapanga iwo kupanga chimodzimodzi m'mene Iye akufunira iwo achite, ndiye musandiuze ine kuti Mkwatibwi sadzamumvera Iye. Musandiuze kuti Mkwatibwi sadzalankhula chinthu chimodzi. Musandiuze kuti Mkwatibwi sadzakhala mu umodzi wathunthu!

Chirombo chotuluka ku phompho ndi kwenikweni mdierekezi. Mulungu akuyenera kuononga kachitidwe ka chipembedzo, ndipo Iye akugwiritsa ntchito nyanga zomwezo zimene zakhala zikuopa kachitidwe ka chipembedzo. Iye amaika m'mitima yawo kuchita izo.

Vesi 18: *"Ndipo mkaziyo unamuona, ndiye mudzi waukulu, wakuchita ufumu pa mafumu a dziko."*

Kodi ndi mzinda uti umene umachita ufumu pa dziko lonse lero? Ndi mpingo, Babulo. Si Roma ngati mzinda. Ngati mzinda Roma sangakhale ndi boma lokhazikika payekha. Akuti mzinda uwu uchita ufumu pa dziko lonse. Kodi ndi mzinda wanji umenewo? Ndi Mpingo wa Roma, koma udzaotchedwa ndi moto.

Kodi mukuchiona chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chiwiri cha bukhu la Chivumbulutso? Ndi kufotokoza kwa bukhu la Ufumu wa Chiroma. Chikuonetsera kumene Ufumu wa Chiroma unayambira. Chikuonetsera chirombo chisanavulazidwe. Chikuonetsera icho pamene chinakhala ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi. Chikuonetsera ngakhale chiononge ko. Mngelo anati, "Yohane, tabwera kuno kamphindi. Ine ndikufuna ndikutengere apa mu Mzimu ndi kukuonetsera chimene chidzachitika kwa hule wakaleyo." **Iye anaotchedwa ndi moto ndi chirombo chomwecho anachikwera.** Iye adzapita ku kusapezeka limodzi la masiku amenewa. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHISANU NDI CHITATU

Tsopano pamene mwapemphero tikuganizira chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chitatu cha Chivumbulutso, tiyeni titenge mavesi asanu oyambirira ndi kuwafananiza iwo ndi Chivumbulutso chaputala 10. Pamene tikuchita izi, tikhoza kuona bwinobwino m'mene Chivumbulutso chaputala 10 chikuchitira ndi chinthu chamoyo chosaoneka cha Mkwatibwi oyeramtima, koma Chivumbulutso chaputala 18 chikuchita ndi Ayuda ndi oyeramtima a ku chisautso amene aitanidwa ndi atumiki wa chiyuda 144,000 pamene iwo akulalikira uthenga ku dziko lapansi. Uthenga udzasunga miyoyo yapamwamba yochuluka kuti isalambire chirombo ndi fano lache.

Uthenga wa 144,000 ukuchenjeza dziko lapansi lonse kuti lisalambire kachitidwe ka mpingo ka mdierekezi. Uthenga wao udzathandizanso anthu kupambana kulowa mu ulamuliro wa mileniamu ngati anthu kudzachulukana pa dziko mu nthawi imeneyo powasunga iwo kuti angatenge chilemba cha chirombo, kapena kupembedza chirombo.

Monga Chivumbulutso chaputala 10 apa chikuonetsera kudzoza kwamphamvu kwa Yesu pa Mkwatibwi, vesi loyamba la Chivumbulutso chaputala 18 likuonetsera kudzoza kwa mphamvu kwa Mulungu pa Ayuda 144,000, kupanga njira ku utumiki wao mu nthawi imeneyo ya m'dima.

Vesi 1: *"Zitatha izi ndinaona mngelo wina wakutsika m'mwamba wakukhala nao ulamuliro waukulu; ndipo dziko linaunikiridwa ndi ulemelero wache."*

Tsopano tiyeni tifananitse Chivumbulutso chaputala 10, vesi loyamba, ndi Chivumbulutso chaputala 18, vesi loyamba. Zaputala zonse cha khumi ndi cha khumi ndi chisanu ndi chitatu chikuonetsera mngelo

akubwera kutsika kumwamba. Chivumbulutso chaputala 10:1 chikumuonetsera Iye ngati *"Mngelo Wankulu."* Chivumbulutso chaputala 18:1 chikumuonetsera Iye ngati mngelo, *"wokhala ndi ulamuliro waukulu."* Chivumbulutso 10:1 akuti, *"Nkhope yake inafanana ndi dzuwa."* Chivumbulutso 18:1 akuti, *"Dziko linaunikiridwa ndi ulemelero wake."* Ndi mngelo yemweyo mu ma chaputala onse. Ndi kudzoza pa Mau, kapena Khristu mu maonekedwe a mngelo, kuonetsera utumiki wa Mkwatibwi ndi kuonetsera utumiki wa atumiki a Chiyuda 144,000 onse. Ngakhale kuti utumiki wa kwa Mkwatibwi ndi wa kwa atumiki a Chiyuda 144,000 ndi osiyana ndi zaka zitatu ndi theka, Khristu akudzoza onse utumiki kugwira ntchito zawo. Chivumbulutso chaputala 18 chikuwalora "oyeramtima amene akugonabe" kudziwa kuti Babulo wasandulika mokhalamo ziwanda. Pali kufananitsa kwina ine ndikufuna ndipange apa pakati pa Chivumbulutso 10:1, kumene kuli **"Nkhope yake ngati dzuwa"** ndi Chivumbulutso 18:1, chimene chiri **"dziko linaunikiridwa ndi ulemelero Wake."** Chivumbulutso 10:1 ndi kwa Mkwatibwi wokhala ndi vumbulutso, pamene Chivumbulutso 18:1 ndi kwa anthu a thupi pa dziko. Ndi uthenga wa 144,000 monga zapangidwa kumveka mu chaputala ichi.

Tsopano tiyeni tipitirize ndi Chivumbulutso 18, chimene chikuchitika Chivumbulutso 10 chitatha ndipo ndi utumiki wa 144,000 umene udzachenjeza dziko kuti lisalambire ku kachitidwe ka chirombo ndipo adzadzutsa a Khristu wobadwanso amene adakali mu kachitidwe ka mpingo.

Vesi 2: *"Ndipo anafuula ndi mau olimba, nanena, Wagwa, wagwa, Babulo waukulu, nasandulika mokhalamo ziwanda, ndi mosungiramo mizimu yonse yonyansa, ndi mosungiramo mbalame zonse zonyansa ndi zodanidwa."*

Vesi 3: *"Chifukwa ndi vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake mitundu yonse idagwa; ndipo mafumu adziko adachita naye chigololo; ndipo ochita malonda a dziko analemera ndi mphamvu ya kudyera kwache."*

Taonani ichi akuti, pakuti mafuko **aledzera,** kutanthauza kuti iwo amwa kale. Izi zikuonetsera nthawi imene Babulo asanaweruzidwe.

Vesi 4: *"Ndipo ndinamva mau ena ochokera kumwamba, nanena, Turukani m'menemo, anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ache, ndi kuti mungalandireko ya miriri yache."*

Vesi 5: *"Pakuti machimo ache anaunjikika kufikira ku m'mwamba, ndipo Mulungu anakumbuka zosalungama zache."*

Mau oti, *"ngati mkango ubangula,"* mu Chivumbutso chaputala 10 ndi vumbulutso la uzimu kwa Mkwatibwi kuti Khristu sakuchitanso mu gawo la chikhristu cha chipembedzo. Taonani kufanana kwa zimene analankhula zokhudza chipembedzo cha bodza mu chaputala cha khumi ndi chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chitatu.

Mngelo uyu amene anafuula mwamphamvu, kunena, *"Wagwa, wagwa Babulo wankulu nasandulika mokhalamo ziwanda,"* **ali ndi zotsatira zimodzimodzi monga kubangula kwa mkango ku Chivumbulutso 10:3, koma kwa anthu ena.** Pa nthawi imene mngelo uyu wa pa Chivumbulutso 18 akubwera, kachitidwe konse ka mpingo kakhwima pa chiweruzo cha Mulungu.

Vesi 6: *"Mubwezere, monganso uwu unabwezera, ndipo muwirikize kawiri, monga mwa ntchito zache; chikhomo unathiramo, muuthirire chowirikiza."*

Mulungu akuyamba kupereka lamulo lapadera, *"Mubwezere monganso iye anabwezera inu, ndipo muwirikize kawiri, monga mwa ntchito zache."* Atumiki a Chiyuda 144,000 adzakhala ndi mphamvu ya Mau kubweretsa chiweruzo pa Babulo. Izi zikuonetsera uthenga umene udzatsutsa Babulo. Ife tikhoza kulalika motsutsa Babulo zonse zimene tingafune ndipo zingothandiza Mkwatibwi. Pali anthu ochepa amene adzazimva ndi kutuluka.

Ine ndikhoza kukuuzani chimene Katolika wa Chiroma ali, ine ndikhoza kukuonetserani mbiri, ndikukuonetserani m'mene analiri mu chivundi mu M'bado wa M'dima, ndi kukuonetserani ochuluka amene awapha; koma Mpingo wa Roma udzapitirira ndi kutukuka. Ine ndikhoza kukuonetserani inu mabungwe onse a Chiprotestanti, kukuonetserani pamene iwo anataya Mau, ndi kulalika motsutsa iwo koma iwo adzapitirira. Chifukwa chiyani? Chifukwa liu liri kwa Mkwatibwi yekha basi tsopano. "Tulukani pakati pawo, anthu anga. Chokani pakati pake." Koma likubwera tsiku Mkwatibwi akachoka pa dziko iri pamene Mulungu akadzakhala ndi liu lotsutsa Babulo zidzagwira ntchito.

Apa pa vesi 6, Mulungu akuyamba kupereka lamulo kubwezera mphotho kwa iye ndi kulengeza chiweruzo motsutsana ndi Babulo. 144,000 awa , mogwirizana ndi Chivumbulutso 14, adzalalikira Uthenga Osatha ndipo adzatsutsana naye Babulo. Iwo adzalalikira ndi kuliuza dziko lapansi cheni cheni chimene Babulo ali. Iwo adzaliuza dziko lapansi cheni cheni chimene ana akazi a chiprotestanti ali. **Akadzatha, adzakhala atalalikira ndi kuulura ku dziko lapansi chimene kachitidwe aka ka hule kali.**

Vesi 7: *"Monga momwe unadzichitira ulemu, nudyerera, momwemo muuchitire chouzunza ndi chouliritsa maliro: pakuti unena mumtima mwache, Ndikhala ine mfumu, wosati wamasiye ine, wosaona maliro konse ine."*

Ndi chimene iye akunena lero. Iye akumverera otetezedwa, koma Mulungu ali ndi chiweruzo chikuyembekezera pa iye. Padzakhala chiweruzo motsutsana ndi iye. Ndi mau a 144,000. Ayuda adzaonetsera dziko lapansi chimene iye ali. Uthenga udzabwereranso ku Israeli monga pa chaputala cha 15 cha Machitidwe, Aroma chaputala cha 11 ndi malemba ochuluka mu Chipangano Chatsopano kuonjezera apa, koma Zakaria, chaputala 12:10-11 ndi chaputala 13:1 chidzakwanira. Ndi chifukwa chake ali ku dziko la kwawo lero. Iwo akuyembekezera aneneri awiri kubwera ndi kuulura kwa iwo kuti kodi Messia ndi ndani. Chaputala cha khumi ndi chinai cha Chivumbulutso chinati, "Iwo sanadetsedwa ndi akazi." Kodi mukudziwa kuti akazi amenewa ndi ndani? Mpingo wa Katolika ndi zipembedzo zina za Chiprotestanti. Iwo amapita ndi kuyesera kutembenuza Ayuda ku zikhulupiriro za utatu, koma tithokoze Mulungu kuti Ayuda sangawalandire iwo. Iwo ali ndi kulingalira kwabwino kusiyana ndi zimenezo. Iwo akudziwa kuti Mulungu anati, *"Imva iwe Israeli, Yehova Mulungu wako ndi Mulungu m'modzi."* Mulungu m'modzi ameneyo anaonekera mu thupi la munthu, kupyolera mwa mwana wake Yesu Khristu.

Vesi 8: *"Chifukwa chache miriri yache idzadza m'tsiku limodzi, imfa, ndi maliro, ndi njala; ndipo udzapserera ndi moto; chifukwa Ambuye Mulungu womuweruza ndiye wolimba."*

Mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chiwiri cha bukhu iri, ife tinakuonetserani m'mene nyanga khumi zidzaweruzire ku kuotcha kachitidwe ka Chiroma. Vesi lotsiriza la chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chiwiri likukamba za mzinda. Akuti, *"Ndipo mkaziyo unamuona, ndiye mudzi waukulu, wakuchita ufumu pa mafumu a dziko."*

Pali mizinda iwiri yotchulidwa mu bukhu la Chivumbulutso. Umodzi mwa iwo ndi Babulo, chimene ndi zimene tikulankhula pano. **Ndi kachitidwe ka mpingo.** Ndi hule wa Chiroma ndi ana ake akazi mahule. Palinso mzinda wina mu machaputala a makumi awiri ndi chimodzi komanso makumi awiri ndi chiwiri a Chivumbulutso, ndipo ndi Mpingo Woona. **Mizinda yonse iwiri ndi mipingo.** Umodzi wa iwo udzalandira kudzoza kwa Mulungu, koma winawo udzaweruzidwa ndi kuotchedwa ndi moto. Kodi inu muli mu uti? Funso labwino, sichoncho?

Kodi mzindawo ndi wa chiyani? Ku Chipangano Chakale pamene mizinda inayamba kumangidwa, anali malo othawirako kokapezera chitetezo kwa adani. Ukakula mzinda, mochulukanso anthu amayang'anira mzinda umenewo pa chisamaliro ndi chitetezo. Zimenezo ndi mu gawo la thupi, koma tikulankhula apa za mzinda wauzimu.

Anthu anati ku Chipangano Chakale kuti Babulo unali mzinda wolimba kwa adani, kuti mukalowamo mukhoza kukhala otetezeka. Ichi ndi chimene amanena pa zokhudza Mpingo wa Katolika wa Chiroma. "Ndi mzinda waukulu. Ndi mpingo waukulu. Bwerani mudzapeze chitetezero cha moyo wanu." Koma Mulungu anati udzagwa. Mu mphindi imodzi udzagwa. Mulungu analankhula mau a chiweruzo motsutsana ndi Babulo, mzinda wa thupi, kupyolera mwa mneneri Yeremiya; iye anagwa ndipo sadzadzukanso.

Chipembedzo chiri chonse cha bodza ndi zamatsenga zimene sizinakhalepo pa nkhope ya dziko la pansi, mzimu wa zimenezo unali mwa Babulo wa thupi. Inu mukhoza kuzipeza mu mbiri kumene ambiri a iwo anachita chigololo pa nthawi ya mapemphero awo. Izo zinali mu thupi. Ziri mu mzimu tsopano. Anthu amachita chigololo ndi mzimu wa otsutsakhristu. Iwo ndi otsutsidwa ndi chigololo, pamene mudzaona powerenga Mau awa a Mulungu, ndipo zafotokozedwa momveka mu bukhu iri.

Tiyeni tipite ku Yeremiya 51. Ine ndikufuna ndikuonetsereni inu pang'ono za mzinda uwu wa thupi ndi chiweruzo cha iwo. Ndiye ndikufuna tibwerere ndikukuonetserani mzinda wa uzimu, Babulo, ndipo walembedwa mu Bukhu la Chivumbulutso. Yeremiya 50 ndi 51 akuchita ndi mzinda wa thupi wa Babulo.

Inu mudzadabwa m'mene zikugwirizanirana ndi mzinda wa uzimu wa Babulo. Apa tikupeza m'mene mbiri ya m'mene mzindawo unagwera.

Tamvetserani ku Mau. Yeremiya 51:6- *"Thawani pakati pa Babulo, yense apulumuke moyo wake; musathedwe mu choipa chache; pakuti ndi nthawi ya kubwezera chilango; Yehova adzambwezera iye mphotho yache."*

Iwo akukhala mu Babulo amati ndi mzinda wotetezeka ndipo sangatengedwe. Iwo amati sungaonongedwe ndipo udzaima ku nthawi za nthawi, koma Mau a Mulungu anadza kupyolera mwa Yeremiya mneneri ndipo iye analankhula mawu a chiweruzo motsutsana ndi mzinda wa Babulo ndipo unagwa.

Kodi zinalankhulidwa zotani zokhudza mzinda wa uzimu*? "Turukani m'menemo, anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ache."* Yeremiya anaima ndi kunenera motsutsana ndi Babulo. Tangoganizani m'mene anamusekera mneneri ameneyo? Mzindawo unali ma mailosi kuzungulira; makoma anali moti simungakhulupirire kutalika ndi okhuthala, ndipo anali ndi gulu la nkhondo lalikulu. Mneneri uyu anaima ndi kunena, "Tulukani mu Babulo, aliyense amene akufuna kuwomboledwa, tulukani mu Babulo." Mau a Mulungu anabwera ndipo iye anagwa . Iye lero ali wakugwa ndipo sadzamangidwanso.

Yeremiya 51:7-8- *"Babulo wakhala chikho cha golidi m'dzanja la Yehova, amene analedzeretsa dziko lonse lapansi; amitundu amwa vinyo wache; chifukwa chake amitundu ali ndi misala. Babulo wagwa dzidzidzi naonongedwa; munkuwire iye, mutengere zowawa zache bvunguti, kapena angachire."*

Kumbukirani kuti Mulungu anati anampatsa iye [Babulo wa uzimu] mpata kuti alape. [Chivumbulutso 2:21] Apa, Mulungu anati kumpatsa mankhwala kuti achier, koma munalibe machiritso mwa iye. Palibe machiritso kwa Babulo wa uzimu. Mpingo wa Katolika wa Chiroma upitirira kuyenda mu njira zache. Iye wapha ndi kupha ndipo sanalape mpakana tsiku la lero. Ngakhalenso Babulo uyu wa thupi sanalapa. Yeremiya 51:9- *"Tikadamchiritsa Babulo koma mumsiye iye, tipite tonse yense ku dziko lache; pakuti chiweruziro chake chifikira kumwamba, chinyamulidwa mpaka ku thambo."*

Yeremiya analankhula Mau a Mulungu, koma iwo sanamvere iwo. **Mpingo, anthu a m'dziko lapansi, mverani Mau anga, "Kanani Babulo!"** Kanani Babulo wa uzimu uyu! Anthu akuti palibe njira iriyonse mzinda waukulu uwu ungatengedwere. Zikuoneka ngati ndikosatheka kutenga mzinda uwu kapena kuuononga. Miyoyo imapita kukapeza chitetezero m'malo mwake kukaonongedwa.

Bukhu la Ahebri likutiuza za mzinda umene inu mukhoza kuthawirako kukapeza chitetezo cha miyoyo yanu. Mzinda ndi malo opezera chitetezero. Pali mzinda pamene pali chitetezo. Kodi mzinda umenewo ndi chiyani? Ndi mzinda wa Yerusalemu Watsopano umene uchokera kwa Mulungu kuchokera kumwamba. Kuli chitetezo kumeneko; koma Babulo adzagwa. Yeremiya 51:10- *"Yehova watulutsa chilungamo chathu; tiyeni tilalikire mu Zioni ntchito ya Yehova Mulungu wathu."* Ndi chimene tikuchita, kulengeza ntchito ya Ambuye. Yeremiya 51:11- *"Nolani mibvi; gwirani zolimba zikopa; Yehova waukitsa mtima wa mafumu a Amedi; chifukwa alingalira Babulo kuti amuononge; pakuti ndi kubwezera chilango kwa Yehova; kubwezera chilango chifukwa cha Kachisi wake."*

Yeremiya 51:63-64- *"Ndipo padzakhala, utatha kuwerenga bukhu iri, ulimange ndi mwala, nuliponye pakati pa Firate; nuti, chomwecho adzamira Babulo, sadzaukanso chifukwa cha choipa chimene ndidzamtengera iye; ndipo adzatopa. Mau a Yeremiya ndi omwewo."*

Pamene tikutenga Chivumbulutso, chaputala 18 kachiwirinso, inu mudzaona mngelo akutenga mwala ndikuuponya mu nyanja ndi kunena, *"Babulo adzapasulidwa kolimba ndipo sadzapezedwanso konse."* Zikulankhula za mzinda wa uzimu wa Babulo ku Chivumbulutso.

Woyenera kubwezera ndi ndani kuononga Babulo? Ndi Ambuye. Kodi iye anaononga bwanji Babulo? Tikuwerenga kuti mulungu adzadzutsa mzimu wa Amedi kubweretsa kubwezera pa Babulo. Mzinda wa ukulu uwu wa Babulo unali ndi mtsinje umene unazungulira makoma ndi kudzera pakati. Zimaoneka ngati kunali kosatheka kuti ankhondo kuti autenge. Iwo amati ndi mzinda wotetezeka, mzinda umene sungagwe.

Ndi chimene iwo akunena lero za Mpingo wa Aroma lero. Iwo akuti ndi umene sudzagwa. Iwo wakhala kwa zaka mazana, koma Mau a Mulungu akulankhula motsutsa iwo. Dikirani mpakana 144,000 alankhule mau a chiweruzo motsutsa iwo. Iye adzagwa; udzagwa pansi.

Taonani kuti Belisazara, mfumu ya Babulo, [mu Bukhu la Danieli], anakonza phwando la akulu ankhondo ake, akalonga, ndi ena. Panabwera dzanja pa khoma: MENE, MENE TEKEL, UFARSIN. Danieli anabwera ndikutanthauzira. Linati, *"Waikidwa pa sikelo ndipo wapezeka woperewera. Usiku uno ufumu wanu udzatengedwa manja mwako ndi kuperekedwa kwa anthu ena."* Pa nthawi yomweyo Belisazara anali pa phwando ndipo cholembedwa chinali pa khoma, Amedi ndi Aperesi anali akukumba tinjira ta madzi kuti mtsinje uyenderere mu mtsinje wakale, ku munsi kwa mtsinje, kotero gulu la nkhondo la Amedi ndi Aperesi anazungulira pansi pa khoma la Babulo, ndipo usiku umenewo Belisazara anapezeka wakufa ali ndi mpeni kumbuyo kwache. Babulo wathupi anagwa kotero adzagwanso Babulo wauzimu.

Mbiri ikutionetsera kuti Mau a Mulungu adzakwaniritsidwa. Iwo amati mzinda sungatengedwe, koma Mau a Mulungu anati, *"Babulo adzagwa."* Iye anachita chiyani? Iye anadzutsa mzimu wa Amedi ndikunena, *"Pitani mukatenge Babulo."*

Chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chiwiri cha Chivumbulutso, vesi 16-18 chikuti, nyanga khumi zinadana ndi Babulo [hule], ndipo Mulungu anaziika mu mtima mwawo kumuotcha iye ndi moto. Chinthu chomwecho chimene chinachitika ndi Babulo mu Chipangano Chakale ngati mzinda wa thupi, chichitika ku Babulo wa uzimu ku Chipangano Chatsopano. **Kachitidwe ka mpingo aka kadzagwa. Kadzaotchedwa ndi moto. Chikatolika chidzafika ku mapeto.** Babulo adzagwa. Kodi iye anagwa ku Chipangano Chakale? Mafuko ambiri ndi mizinda inalumikizana naye chifukwa cha chitetezo. Chifukwa chiyani? Babulo anali ndi chuma, malonda, ndi ndalama. Zikuoneka ngati zonse munthu amafuna zakuthupi zinali ku Babulo, koma Mulungu sanali m'menemo, Iye sali ngakhale mu Babulo wauzimu.

Tiyeni tichite ndi Babulo wauzimu mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chitatu cha Chivumbulutso. Pamene papa adzapanga pangano ndi mafuko ambiri, zidzaoneka ngati zonse zimene munthu akhoza kuzifuna zikhoza kudzapezeka mu kachitidwe ka Babulo uyu. Kadzatenga ulamuliro pa golidi pa dziko lapansi, kachitidwe ka nkhondo, kachitidwe ka ndalama, ndi zonse. Padzakhala kachitidwe ka gulu limodzi la nkhondo pa dzikolonse ndi kachitidwe ka ndalama imodzi pa dziko lonse. [Ine ndikulankhula za dziko la uneneri. Izi sizikukhudza Kutali Kum'mawa.]

Dziko lapansi lidzadabwa ndi chirombo [Chivumbulutso 13:3] chimene bala lake linapola. Pamene kachitidwe ka Chiroma kakubweranso ku mphamvu mu tsiku lotsiriza, dziko lidzati chinthu chimenecho ndi Mulungu ndi chinthu chachikulu chimene sichinakhalepo. Iwo adzathawira ku Babulo kukapeza chitetezero ku miyoyo yawo, koma Mau a Mulungu alankhula motsutsana ndi izo.

Pa nthawi yomweyo Mpingo wa Katolika wa Chiroma ukulamulira Ulaya, pali mzimu wa chikominisiti kumangika mu mafuko khumi omwewo. Chikominisiti [mtundu wa ku Ulaya] udzadzuka ndi kuononga Roma monga m'mene Mulungu wanenera. Zidzachitika; Mau sangalephere.

Vesi 9: *"Ndipo mafumu a dziko ochita chigololo nadyerera naye, adzalira nadzalira maliro pamene aona utsi wa kutentha kwache, poima patali."*

Vesi 10: *"Chifukwa chakuopa chizunzo chache, nanena, Tsoka, tsoka, mudzi waukuluwo ndi wolimba! Pakuti mu ora limodzi chafika chiweruzo chanu."*

Mafumu amene anadabwa naye si mafumu khumi aku Ulaya amene amadana ndi hule, ndi kumutentha iye ndi moto. [Chivumbulutso 17:16] Awa ndi mafumu amene akunyengedwabe mpakana pano. Mafumu khumi a chikominisiti adzasangalala pamene amuotcha iye. *"Ataima patali"* zikutanthauza kuti mafumu amene achita naye chigololo mu Madera adziko kupatula nyanga khumi za ku Ulaya. Pa nthawi iyi Babulo adzaonongedwa. Iye adzatsitsidwa; iye nadzagwa mu gawo lotsiriza la sabata la 70 la Danieli, Mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye asanabwere ku dziko.

Vesi 11: *"Ndipo ochita malonda a m'dziko adzalira nadzauchitira chifundo, popeza palibe munthu agulanso malonda ao."*

Mu chaputala chachisanu ndi chimodzi cha bukhu iri, ife tinaphunzira za mzimu wa otsutsakhristu. Panali liu limene linapfuula, *"Muyeso wa tirigu wogula lupiya; ndi miyeso itatu ya balele yogula lupiya; ndi mafuta a vinyo usaziipse."* Kodi ogulitsawo ndi ndani? Ndi zonse kuthupi ndi uzimu. **Ogulitsa malonda amene akugulutsa chipembedzo cha Katolika wa Chiroma ndi amsembe ovala mikanjo, pamene akupita kuchokera ku dziko kupita ku dziko kugulitsa chiphunzitso cha bodza.** Iwo

amagulitsa mgonero, ndipo iwo amapanga misa ku zimenezo. Chirichonse ndi chopezera ndalama mu kachitidwe kameneko.

Osati zokhazo, mu mumasiku awa otsiriza, Mpingo wa Katolika wa Chiroma wasandulika umodzi wa mabungwe a chuma chambiri pa dziko lonse lapansi. Iye ali ndi ma billion a ma dollar, mu ngwirizano, makapani, ndi zina zotero.

Pamene iye anali pa mpando mu M'bado wa M'dima, iye amatha kuitanitsa chisokonezo ndipo aliyense wa Katolika wa Chiroma amatha kuopa. Iye akubweranso ku malo amenewo kachiwirinso, ndipo monga abwezeretsedwa adzapangitsa mtundu wa anthu, onse akulu ndi ang'ono, kutenga chilemba. Iye adzakhala ndi njira zokokera zingwe; ndipo fano la chirombo lidzakhala momwemo ndi icho.

Kodi mukuona Mpingo wa Aroma wa tsopano? Mukuona m'mene aliri ndi ulamuliro wa ndalama ndi chirichonse? Koma Mau a Mulungu alankhulidwa motsutsana ndi iye ndipo iye adzagwa.

Vesi 12: "*Malonda a golidi, ndi siriva, ndi a mwala wa mtengo wache, ndi ngale, ndi nsalu ya bafuta, ndi a chibakuwa, ndi a yonyezimira, ndi a mlangali; ndi mitengo yonse ya pfungo lokoma, ndi chotengera chirichonse cha minyanga ya njobvu, ndi chotengera chirichonse chamtengo wa mtengo wache wapatali, ndi cha mkuwa ndi chachitsulo, ndi cha msangalabwi."*

Iye wakhudzidwa ndi malonda ochuluka. Zina za izi zikuimirira zinthu za uzimu. Chibakuwa, mlangali, ndi miyala yonse ya mtengo wapatali ndi momwemo m'mene mkaziyu anadzikometsera. Sikungoti iye akukhudzidwa ndi malonda a dziko lapansi okha, komanso akugulitsa chiphunzitso chake ku dziko lapansi.

Vesi 13: "*Ndi kinamomo ndi amomo, ndi zofukiza, ndi zodzola, ndi libano, ndi vinyo, ndi mafuta, ndi ufa wosalala, ndi tirigu, ndi ng'ombe, ndi nkhosa, ndi malonda a kavalo, ndi amagareta, ndi a anthu ndi a miyoyo ya anthu."*

Iye akugulitsa miyoyo ya anthu. Anthu ambiri agulitsa miyoyo yawo ku kachitidwe ka Chiroma, adzati pozadzuka ndi kupeza kuti atayika. Amsembe amanena mapemphero awo, ndi kuyesa kuwapempherera anthu kuchoka ku "pirigatore." Palibe malo amenewo. Miyoyo ya anthu iri mu ukapolo wa kachitidwe kameneko. Iye ndi hule. Ndi chimene Baibulo likunena, ndipo ana akazi ndi mahule. Ndi kachitidwe aka ka chipembedzo.

Kochuluka kwa kotsatira kwa chaputala ichi ndi kodzifotokozera kokha ndipo kukuonetsa malonda Mpingo wa Katolika ukuchita, mu ora lotsiriza monga tafotokoza kale tisanawerenge mavesi otsalawa; amene akuonetsa kudabwa kwa anthu osamva pa zimene zinachitika.

Vesi 14: "*Ndipo zokhumbitsa moyo wako zidakuchokera; ndipo zonse zolongosoka, ndi zokometsetsa zakutaikira, ndipo izi sudzazipezanso konse."*

Mpingo uwu ukugwa. Zipembedzo zonse zidzafika ku mapeto ndi kugwa kwa Mzinda Vatican.

Vesi 15: "*Otsatsa izi, olemezedwa nao, adzaima patali chifukwa chakuopa chizunzo chache, nadzalira, ndi kuchita chifundo."*

Vesi 16: "*Nadzanena, Tsoka, tsoka mudzi waukulu wobvala bafuta ndi chibakuwa, ndi mlangali, wodzikometsera ndi golidi ndi mwala wa mtengo wache, ndi ngale!"*

Vesi 17: "*Pakuti mu ora limodzi chasanduka bwinja chuma chachikulu chotere. Ndipo watsigiro aliyense, ndiyense wakupita pa pakutipakuti, ndi amalinyero, ndi onse amene amachita kunyanja, anaima patali."*

Vesi 18: "*Napfuula poona utsi wa kutentha kwache, nanena, Mudzi uti ufanana ndi mudzi waukuluwo?"*

Vesi 19: " *Ndipo anathira pfumbi pamitu pao, napfuula, ndi kulira, ndi kuchita maliro nanena, Tsoka, tsoka, mudzi waukuluwo, umene analemekezedwa nawo onse akukhala nazo zombo panyanja, chifukwa cha kulemera kwache, pakuti mu ora limodzi unasanduka bwinja."*

Vesi 20: "*Kondwera pa iye, m'mwamba iwe, ndi oyera mtima, ndi atumwi, ndi aneneri inu; chifukwa Mulungu anauweruzira kuweruzidwa kwanu."*

Kumwamba kukukondwera podziwa kuti mzinda uwu umene wapha ndi kuika ku imfa mamilioni udzafika ku kulephera.

Vesi 21: "*Ndipo mngelo wolimba ananyamula mwala, ngati mphero yaikulu, naiponya m'nyanja, nanena, Chotero Babulo mudzi waukulu, udzapasulidwa kolimba, ndipo sudzapezedwanso konse."*

Kodi ife tinawerenga chiyani za mzinda wathupi wa Babulo? Yeremiya anatenga bukhu lofunyulura, ndi kumangirako mwala kwa ilo, ndi kuliponya mu mtsinje, ndi kunena, *"Chotero Babulo mudzi waukulu, udzapasulidwa kolimba, ndipo sudzapezedwanso konse."* Kodi mzinda wa thupi wa Babulo unaonongedwa? Inde, unatero. Ndipo Babulo wa uzimu adzaonongeka; ndipo kutaya mwala mu nyanja kukuimirira chimene Mulungu adzachite. Mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chimodzi cha Chivumbulutso, vesi 17-18, Mau a Mulungu akulankhula za chivomerezi chimene chidzachitike pamene Mulungu atsiriza chiweruzo chake ku kachitidwe ka dzikolapansi.

Vesi 22: *"Ndipo mau a anthu oyimba zeze, ndi a woimba, ndi oliza zitoliro, ndi a oomba malipenga sadzamvekanso konse mwa iwe; ndi mau a mphero sadzamvekanso konse mwa iwe."*

Vesi 23: *"Ndi kuunika kwa nyali sikudzaunikiranso konse mwa iwe; ndi mau a mkwati ndi mkwatibwi sadzamvekanso konse mwa iwe; pakuti otsatsa malonda anu anali omveka a m'dziko; pakuti ndi nyanga yako mitundu yonse inasokeretsedwa."*

Apa akuti *"Kuunika kwa nyali sikudzaunikiranso konse kwa iwe,"* kutanthauza kuti kudzakhala m'dima okhaokha. *"Ndi mau a mkwati ndi mkwatibwi sadzamvekanso konse kwa iwe."* Kuziphatikiza zonse, zatha, ndi nthawi ya chiweruzo. Gawo lotsiriza la vesi iri likuti, *"Pakuti otsata malonda anu anali omveka a m'dziko."* Iwo ndi amsembe wovala mikanjo amene amagulitsa chiphunzitso chabodza cha mzinda uwu wokometseredwa ndi chibakuwa ndi ngale ndi zina. Mpingo wa Katolika wa Chiroma umadzikongoletsa okha ku masiku otsiriza. Iye akukongoletsa zipata zake lero. **Iye akuitanira ana ake akazi amene sakumumvera kuti abwere ku nyumba. Ndi chimene bungwe la mgwirizano wa mipingo unali. Ndikuwaitana ana akazi kubwerera kwa mai Roma.** Iye akukongoletsa zipata zake. Iye akunena kuti ali otetezeka m'menemo…, kotero bwererani ana akazi inu!

Komanso, Katolika wa Chiroma amati ndi wotetezeka ku chikominisiti. Iye walephera nkhondo iriyonse imene anamenya ndi chikomunisiti. Ndi chimene nkhondo ya Veit Nam inali.

Kumwera kwa Viet Nam kunali kokhako kolimba ndi chikatolika Kutali Kum'mawa, koma tsopano kuli pansi pa hamala ndi zenga kukwaniritsa Mau a Mulungu. Chinachitika ndi chiyani? Chikominisiti chinalowa ndikuzula Chikatolika, Chibudda, ndi china chiri chonse, chifukwa zanenedwa kuti onse Kutali Kum'mwawa adzakhala pansi pa hamala ndi zenga, pamene mafumu akum'mawa akukonzekera nkhondo ya Armageddoni.

Koma Katolika wa Chiroma akukongoretsa zipata zake ndi kuti, "Bwerani mujoyine. Tiyeni tibwere pamodzi ndi kudziteteza ku chikominisiti." Koma iye waluza nkhondo iriyonse imene adamenyapo ndi chikominisiti.

Lotsatira la vesi 23 likuti, *"Pakuti ndi nyanga yako mitundu yonse inasokeretsedwa."* Katolika wa Chiroma wanyenga gawo lalikulu la dziko la kumadzulo ndi nyanga zake, ndi kuchenjera kwake, ndi zochitika, ndi kudzinenera kwake kupempherera kuwatulutsa ku purigatori, powamangira ma sukulu, ndi ziphunzitso zabodza, ndi zophunzitsa zake.

Vesi 24: *"Ndipo momwemo munapezedwa mwazi wa aneneri ndi oyeramtima, ndi onse anaphedwa pa dziko."*

Kodi mukuona chifukwa ine ndi kutsutsana ndi chikatolika? Kodi mukuona chifukwa ine ndikutsutsana ndi ana ake akazi a chiprotestant? **Mzimu womwewo umene unapha oyeramtima amenewo mbuyomo udakali pa anthu, ndipo iwo ndiokonzeka kuika ku imfa iwo amene akuima pa Mau mu ora lino.**

Yeremiya, mneneri, anati Babulo adzagwa ndipo anthu atuluke ndi kudzipulumutsa okha. Uwo unali mzinda wa thupi. Kodi unagwa? Kodi unaonongedwa? Inde. Tazionetsa izi mu chaputala cha khumi ndi chinai vesi limene linati, *"Babulo wagwa wagwa."* Ndi Babulo wa uzimu.

Awa ndi 144,000 alaliki a Chiyuda kulalikira motsutsana ndi Babulo. Tikuonetserani Uthenga umene iwo akulalikira mu m'bado wosapembedza umene tikukhalamo. Chivumbulutso 14:6-8- *"Ndipo ndinaona mngelo wina alikuuluka pakati pa mlengalenga, wakukhala nao Uthenga Wabwino wosatha, aulalikire kwa iwo akukhala padziko, ndi kwa mtundu uliwonse ndi pfuko ndi manenedwe ndi anthu, ndikunena ndi mau akulu, Opani Mulungu, mpatseni ulemerero; pakuti yafika nthawi ya chiweruzo chache; ndipo mlambireni Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi kasupe ndi madzi. Ndipo anatsata mngelo wina nzache ndi kunena, Wagwa, wagwa, Babulo waukulu umene unamwetsako mitundu yonse ku*

vinyo wa mkwiyo wa chigololo chache." Kodi mukuona chimene uthenga udzakhale? Babulo wagwa. Pali 144,000 amene adzaitana chiweruzo motsutsana ndi Babulo. Iye adzaonongedwa. Iye adzagwa. Pamene adzagwa, zimenezo zidzachitika ndi bumgwe la chipembedzo. **Pamene Babulo agwa, ana akazi achiprotestant adzapita naye limodzi ku kugwa. Amen.**